

# MBEWU YA SERPENTI



... Mulungu, Mulungu wamkulu ndi wamphamvu, Amene anapanga zinthu zonse mwa mphamvu ya Mzimu Wake; ndipo wabweretsa Yesu Khristu, Mwana Wake yekhayo wobalidwa, Amene anafa mwaulere chifukwa cha ife ochimwa, Wolungama chifukwa cha osalungama, kuti atiyanjaniitse ife kubwerera kupita mu chiyanjano chopambana ichi chimene ife tiri nacho kachiwiri ndi Mulungu. Monga ife timaphunzitsidwa mu Mawu odala, kuti ife tinali nacho chiyanjano ndi Iye asanakhalepo maziko a dziko. “Pamene nyenyezi za mmawa zinayimba palimodzi, ndipo ana aamuna a Mulungu anafuulira mwa chisangalalo, kutali mmbuyo asanakhalepo maziko a dziko.” Momwe ife tikudziwira kuti iyo siyinali nthawi imene Mwanawankhosa anaphedwa; imene Mulungu, mu kulingalira Kwake kwakukulu, anatiwona ife tikufuula ndi kusangalala mu chipulumutso chathu kupyolera mwa Yesu!

<sup>2</sup> Ndipo, usikuuno, ife tangokhala nako kulawiratu kwa ulemero wawukulu Waumulungu uwo umene uti udzawulidwe pa kudza Kwake Kwachiwiri. Matenda onse ndi chisoni zidzakhala atathana nazo zitapita. Ndiye ife tidzakhala nalo thupi monga thupi Lake laulemerero Lomwe, pakuti ife tidzamuwona Iye monga Iye aliri. Pano pamene ife tikuyang’ana pa manja athu akufota, tsitsi lathu likusanduka lotuwa, ndipo mapewa akugwa, ife tikuzindikira kuti ife ndife zivundi ndipo talunjika wopita ku fumbi kumene mitu yathu yaweramirako tsopano, ndi kumene ife tabwera kuchokerako. Koma, Ambuye Mulungu, motsimikiza basi monga Inu muli Mulungu, Inu munapanga lonjezo kuti ife tidzawukitsidwa kachiwiri mu masiku otsiriza, ndipo ife tikukhulupirira zimenezo.

<sup>3</sup> Mwakachetechete ife tikuyima ndi chikhulupiriro chathu usikuuno mu Kukhalapo Kwanu, tikubwera ndi kulimbamtima chifukwa kuti Yesu anatipempha ife kuti tizichita izo. Osati pa chinthu chabwino chirichonse chimene ife tachita, pakuti ife palibe kanthu tachita kabwino; koma ife tikubwera modzichepetsa, kudzinenera kuti ife tiri nacho chuma ichi chifukwa cha chisomo Chake chimene chaperekedwa kwa ife. Chotero, ife tikubwera kupempha kuti Inu mudzatalitise ife usikuuno mu kubweretsa kwa Mawu. Pakuti izo zalembedwa, kuti, “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Ndipo mulole kamwa ya Mulungu ikhale itayankhula usikuuno. Mulole mawu abwere pamene, ndipo mulole Iwo apite mwakuya mu mitima ya ife, omvetsera, ndi kukhala odzazidwa nawo Mzimu Wanu ndi Kukhalapo Kwanu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>4</sup> Le—lero ndi dzulo, usiku watha, kani, ndipo lero, ife takhala tikuyankhula pa phunziro, poyamba, kuti tiwupatse iwo mutu, *Chifukwa Chiyani Ife Sitiri Chipembedzo*. Ndipo ife tazipanga izo molimbirapo, chifukwa chimene ife sitiri chipembedzo, ndi chifukwa chimene ife sitimakhulupirira mu zipembedzo. Chifukwa, ife tikuzipeza izo mu Baibulo, kuti zipembedzo sizinakonzedwe konse ndi Mulungu; izo zinakonzedwa ndi mdierekezi; ndipo tinatsimikizira izo mwa Baibulo. Ndi momwe kuti, kupyolera mu zipembedzo, akubweretsa pamenepo cholakwitsa. Tsopano ife tiri kunena izi kuti tikonze ndi kuti tibweretse kachisi uyu kulowa mu chiyanjano pozungulira Mawu odala a Mulungu. Kutu, ziyembekezero zathu sizinamangidwe mu zimene chipembedzo chimanena, kapena chimene munthu aliyense amanena; izo zamangidwira pa chimene Ambuye Mulungu ananena. Ndipo ndiyo njira yokhayo imene ife tingakhoze konse kukonzedwa molondola.

<sup>5</sup> Ndipo mmawa uno, ine ndinali nazo zisanu, ine ndikukhulupirira, nkhani zosiyana zimene zatuluka kupyolera mu chipembedzo, zimene ziri mwamtheradi zosati zinayankhulidwa mu Baibulo, zimene mipingo ya Chiprotestanti ikuweramirako, ndi kumaphunzitsa mwa chiphunzitso; chinthu chomwecho chimene manthu wakale wa wachiwerewere, mpingo wa Katolika ukulalikira, ndi kutulukira mu mpingo wa Chiprotestanti. Ndipo ife tikuweramira ku chinthu chomwecho chimene chiri chosiyana ndi paliponse mu Mawu a Mulungu.

<sup>6</sup> Mpingo woyamba wa chipembedzo, ife tinaziyang’ana izo madzulo ano mu mbiriyakale ya makolo a Nicene, ya mpingo wa Nicene. Itachitika imfa ya atumwi, kumeneko chimene chinadzakhala makolo a Nicene, ndipo iwo anapitirira nazo kwa zaka zingapo. Zaka mazana atatu makumi awiri ndi zisanu, potsiriza anabwera ku—ku Nicaea, France, kumene iwo anali ndi—khonsolo yayikulu ya Nicene. Ndipo mkati mmenemo iwo anapanga mbalume izi zimene mpingo wa Katolika uli nazo tsopano, ndiponso izo zaperekedwa mmusi kwa Achiprotestanti.

<sup>7</sup> Ndipo monga ine ndinanena mu—mu kuphunzitsa mmawa uno, umodzi uliwonse wa mibadwo ya mpingo iyo, mpakana ku uwo—ku m’badwo wa mpingo wa Tesalonika uwo, zaka mazana khumi ndi zisanu za mibadwo ya mdima, uko kunalibe nthawi imodzi koma imene Iye anati, “Inu mukadali nalobe Dzina Langa.”

<sup>8</sup> Ndipo pa mbali yina iyi, iwo sanali mwa Khristu panonso, iwo anatuluka mu dzina la chipembedzo, “Katolika, Lutera, Wesile, Baptisti, Presbateria, Pentekoste,” mpaka pansu.

<sup>9</sup> Koma basi kusanachitike kutseka kwa m’badwowo, Iye anati, “Ine ndayika patsogolo panu khomo lotseguka.” Mukuona? Ndipo ndiwo m’badwo umene ife tikukhulupirira

ife tiri mmenemo pakali pano, m'badwo wa khomo-lotseguka, pakati pa kutuluka kotsiriza kwa mpingo wa Laodikaya.

<sup>10</sup> Ndipo ndizo chimodzimidzi zaka mazana atatu makumi awiri ndi zisanu mpaka ku khonsolo ya Ulaodikaya. Ndipo mkati mmenemo iwo anatengera mawonekedwe awa monga ngati kukonkha, kutsanulira, ndi maubatizo abodza, mzimu woyera wabodza, zinthu zina zonse izi. Iwo anatengera izo.

<sup>11</sup> Ndiyeno pamene Lutera, pokhala wansembe, ndipo anatuluka kuchokera mu mpingo wa Katolika, anabweretsa zinthu izi limodzi nazo. Ndipo kuchokera uko kunadza Zwingli, kuchokera mwa Zwingli kunadza Kalvini, kuchokera mwa Kalvini kunadza Wesile, o, mpaka pansi. Ndipo iwo amangopitirira kumabweretsa mbalume zimenezo mmusi. Ndipo Mulungu angakhoze bwanji kuwutsogolera Mpingo Wake, pamene iwo akutsatira misewu imene ngakhale Iye sanayibweretse nkomwe kuti iwo azitsogoleredwa pa iyo?

<sup>12</sup> Ndipo kumbukirani, mu Chivumbulutso 17, ife tinapeza “mkazi.” Tsopano mawu awa ali omveka. Iwo alembedwa mu Baibulo, kotero ine ndikuganiza ine ndikhoza kuwanena iwo. Iwo anati mkazi uyu anali “hule.” Izo zikutanthauza kuti iye anali mkazi wa mbiri-yoyipa; kuti iye amayenera kuti akhale atakwatiwa kwa mwamuna, ndipo akumachita ziwerewere ndi dziko. Ndipo iye anali...Iye anali “MAYI WA TIMAHULE,” chotero iye anali ndi ana aakazi. Ndipo ife tinajambula izo mwachirengedwe, pokhala mu...Ndipo mmenemo, inemwini, kuziwona izo mu Lemba, kuwona ziphunzitso zake ndi chirichonse, ine ndikukhulupirira kuti Ambuye aziyika izo mwangwiro pa mzere, kuti izo sizingakhoze kukhala china chirichonse koma mpingo wa Katolika. Ndiyo njira yokhayo imene izo zingakhoze kukhalira. Ndipo kodi iye anapereka kubala kwa chiyani? Mipingo ya Chiprotestanti. Chimodzimidzi, iye anatero.

<sup>13</sup> Ndipo iye anali nacho mu dzanja lake chikho cha vinyo wa ziwerewere zake, ndipo iye anali kuchipereka icho kwa mafumu a dziko lapansi. Ndipo iye anali wolamulira wa pa dziko lapansi lonse, kuyankhula mwauzimu. Ndipo ndiko kulondola chimodzimidzi. Palibenso wina...

<sup>14</sup> Penyani, tiyeni, ife tikhoza kubwerera mmbuyo kwa Daniele ndi kukatenga fano. Kuliyang'ana fanolo: mutu wa golide, ufumu wa Chibabeloni; mkuwa...kapena siliva, Medi-o-Persia; mkuwa, Alikizanda Wotchuka, ndi ena otero, ufumu wa Agriki; kenako maufumu Achiroma, Roma Wakummawa ndi Wakumadzulo, mapazi awiri.

<sup>15</sup> Ndipo zindikirani mu maufumu khumi awa, amene chimodzimidzi akubwera ndi nyanga khumi izi zimene ife tinali kuzikamba mmawa uno, mu uliwonse wa maufumu khumi awo amene anali oti awuke, uko kunali chitsulo ndi

dongo zitasakanizika limodzi. Ndipo chitsulo icho chinabwera kuchokera ku miyendo, amene anali Roma. Ndipo uko kuli msempha wa Chiroma utasakanizika mu fuko lirilonse limene liripo pansi pa Kumwamba, kupyolera mu mpingo wa Katolika. Ndiko kulondola chimodzimodzi. Ndipo izo sizikanakhoza kusakanizikana, paliponse.

<sup>16</sup> Ndipo iwo ali kukwatirana mosakanizana, pakati pa wina ndi mzake. Baibulo linati iwo akanatero. Ndipo yang'anani pa iwo lero. Mnyamata wanu akamayenda ndi msungwana wa Chikatolika; pamene iwo afika poti akwatirane, iwo ayenera kulonjeza kuti alera ana awo mwa Katolika; mwaona, konsekonse. Onani, ndiko kuti aswe mphamvu ya winayo.

<sup>17</sup> Koma ndi chiyani icho? Baibulo limachitcha chinthu chonsecho kuti ndi chachiwerewere. Tsopano kodi inu muchita chiyani? Ndiko kulondola. Ndipo momwe machimo a anthu ati adzachezeredwe. . .Ife tinabwerera mu Deuteronomo, kuti tisonyeze kuti mwana wapathengo, mwana wamchigololo, sakanakhoza nkomwe kulowa mu msonkhano wa Ambuye kwa mibadwo khumi ndi inai. Izo zinali pansi pa lamulo. Ndipo Khristu anabwera kuti adzakulitse lamulo. Ndi mochuluka bwanji momwe izo ziliri tsopano?

<sup>18</sup> Ndipo ndi chiyani chikuchitika kwa awa, chavuta ndi chiyani ndi adama aang'ono awa pa msewu lero, akazi aang'ono okhwewa-ndudu awa, ndi ovala-zazifupi, adama aang'ono a tsitsi lodula, ndi zina zotero? Chavuta ndi chiyani ndi izo? Ndi chifukwa chakuti mayi wawo ankachita monga choncho. Izo zachezera, kusaweruzika, kuchokera ku m'badwo umodzi kupita ku umzake. Ndicho chimene icho chiri. Ndipo kodi ife tiri ndi chiyani? Ife tafipa pa malo, kungokhala chisakaniziko sikanthu koma nyansi za tchimo.

<sup>19</sup> Ndicho chifukwa Mulungu wawutsa Russia, kutsidyako, ndi bomba la atomiki kuti akalisesepo ilo, monga kusefukira kwa chigumula kunaliri, pamene Iye anakweza mitambo. Zedi, Iye watero. Ndipo Baibulo likunena choncho. Russia, dziko lachikunja monga iwo aliri, achikunja, achita mwamtheradi kusewera chimodzimodzi basi mu manja a Mulungu Wamphamvuzonse. Basi monga Mfumu Nebukadinezara anali woti awononge Israeli chifukwa chakuti iwo analephera kuyenda ndi Mulungu, Russia akuwuka kumene apo kuti “abwezerere oyera,” a mpingo wa Chikatolika, pa magazi amene iye wakhetsa a oyera. Baibulo linanena chomwecho. Iye atenga chinthu chonsecho.

<sup>20</sup> Kotero penyani apa, ngati mayi wawo anali msungwana wa makolasi, ndipo agogo awo akazi, ndi mayi awo anali wadama, kodi iye ali chiyani lero? Wakwasakwa wadolola ndi kuvula. Ana ake adzakhala chiyani?

Ndipo inu mukuti, “Kodi Mulungu amachita zimenezo?”  
Inde, bwana.

<sup>21</sup> Mulungu amachezera kusaweruzika kwa ana, m’badwo, ngakhale mpaka mibadwo khumi ndi inai. Ndipo ngati Khristu anabwera kudzakulitsa, ife tinganene kuti, “Mibadwo zana, kapena mibadwo mazana asanu.” Bwanji, Iye anati, “Two akale, inu munawamva iwo akuti, iwo a nthawi yakalewo, ‘Inu musati muzipha.’ Ine ndikuti kwa inu, yense amene ati amukwiwiyire m’bale wake, popanda chifukwa, wapha kale. Inu mwawamva iwo akunena, iwo a nthawi zakalewo, ‘Inu musati muzichita chigololo.’ Koma ine ndikuti, amene ayang’ana pa mkazi kuti amukhumbire iye, wachita chigololo kale ndi iye.” Iye anapanga izo. . . Kukulitsa ndi chiyani? Kuchipanga icho kukula nthawi zambiri. Ndipo ngati pansu pa lamulo izo zinali mibadwo khumi ndi inai, ndi motalika bwanji momwe chinthu chomwecho chiti chitenge lero?

<sup>22</sup> Ndipo mnyamata, ndi mwamuna wa usinkhu-wapakati, ndi amuna okwatira alibe konse kulemekeza kwa malumbiriro awo a chikwati. Bwanji, iwo amangotenga akazi ndi kumagona nawo iwo paliponse, ndipo monga ngati agaru wamba. Garu ali nako kulemekeza kwabwinoko ndi makhalidwe abwinoko kuposa omwe anthu ena ali nawo. Ndipo ine ndikudziwa kuti ndi zaukali kwambiri, koma ndiko kulondola.

<sup>23</sup> Chifukwa chiyani? Ndipo mipingo ikupita motsatira kumene ndipo sakunena kanthu za izo. Chifukwa chiyani? Iwo akungochita monga mayi wawo amachitira. Mipingo yatengera izo. Chifukwa, mpingo ndi mpingo wa Chiprotestanti uwu unabwera kuchokera mu mpingo wa Katolika, machimo a mpingo wa Katolika achezera pa Achiprotestanti. Ndithudi, izo ziri, kotero m’phika sungakhoze kutcha ketulo “kuda”. Ndi chimodzimodzi zoonaa.

<sup>24</sup> Tsopano ife tikuzipeza, ndipo mu Lemba, ife tinazipeza. . . Ndipo ine sindinakawone konse kolembedwa pa tebulo apa usikuuno. Ine ndinati, mudiwonetse ine malo amodzi pamene Mulungu anayamba wadzozapo chipembedzo. Mudiwonetse ine malo amodzi pamene Mulungu anayamba wadzozapo mlaliki wamkazi. Mudiwonetse ine malo amodzi pamene Mulungu anayamba wadzozapo kukonkha. Mudiwonetse ine malo amodzi pamene Mulungu anayamba wadzozapo kutsanulira. Mudiwonetse ine malo amodzi pamene Mulungu anayamba wakhala naye aliyense atabatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Pezani zinthu zimenezo. Ndipo komabe ife mowirikiza timachita zimenezo. Izo ziri kumene mu mpingo monse. Tsopano, ine ndinati, “Njira yanu. . .”

<sup>25</sup> Chifukwa chimene ife sitikanakhoza kukhala Achibaptisti, chifukwa ife timakhulupirira mu kubatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Palibe mmodzi anayambapo, mu Baibulo,

anabatizidwa mwa njira yina iliyonse. Inu mukandiwonetsa ine malo amodzi pamene munthu mmodzi anabatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” ine ndikweza manja anga ndi kunena kuti ine ndine mneneri wabodza.

<sup>26</sup> Ndipo ngati Baibulo limanena kuti inu muyenera “kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu,” izo zikutanthauza kuti inu muyenera kuzichita izo mwa njira imeneyo. Paulo anawalamulira iwo kuti abatizidwe kachiwiri. Ziribe kanthu momwe iwo anali atabatizidwira, iwo amayenera kubwera, kuti adzabatizidwe kachiwiri. Iwo anabatizidwa ndi munthu yemweyo amene anamubatiza Yesu Khristu; Yohane Mbatizi. Iye anati, “Izo sizigwirira ntchito panonso. Inu muyenera kubwera, kuti mudzabatizidwe kachiwiri.” Ndipo iwo amayenera kuti achite zimenezo iwo asanalandire Mzimu Woyera. Ilo linali dongosolo la Mulungu.

<sup>27</sup> Ine ndikhoza kupita mwakuya pang’ono kuposa pamenepo, usikuuno. Chifukwa chiyani? Yesu amasunga Mawu Ake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Tsopano, pafupifupi nonse a inu munali muno mmawa uno, koma ine ndikufuna kuyala pang’ono moonjezeranso pa izo.

<sup>28</sup> Bwanji Paulo anatuma, kulumulira izo zitachitika kale? Paulo anati, “Ngakhale ngati Mngelo wochokera Kumwamba atabwera ndi kulalikira china chirichonse, msiyeni iye akhale wotembereredwa.”

<sup>29</sup> Tsopano inu mukuti, “Ife tiri nako Kuwala kwatsopano pa izo.” Ayi, inu mulibe. Ndicho chimene mdierekezi anadza nacho kwa Eva, Kuwala kwina kwatsopano. Simukusowa Kuwala kwatsopano ayi. Inu mukusowa kuyenda mu Kuwala kumene Mulungu wakuyika kale apa, ndizo zonse.

<sup>30</sup> Tsopano penyani izi, kuphweka kwake chabe. Pamene iwo anabwera pansu kuchokera ku Phiri Lachiwalitsiro, Yesu anati, kwa ophunzira Ake, “Kodi anthu amati ine Mwana wa munthu ndine yani?”

“Wina akuti Inu ndinu ‘Mose, kapena Eliya, mmodzi wa aneneri.’”

Iye anati, “Inuyo mukuti ndi ndani?”

<sup>31</sup> Iye anati, Petro anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

<sup>32</sup> Iye anati, “Wodala ndiwe, Simoni, mwana wa Yonasi; pakuti thupi ndi magazi sizinawululire izi kwa iwe.” Mukuona, izo sizimabwera kupyolera mu maseminare. Izo sizimabwera kupyolera mu zipembedzo. “Thupi ndi magazi sizinawululire izi kwa iwe. Iwe sunaziphunzire izo konse kupyolera mu sukulu iliyonse ya zamulungu. Koma Atate Anga, amene ali Kumwamba, awulula izi kwa iwe. Ndipo pa thanthwe ili ine ndidzamangapo Mpingo Wanga; ndipo zipata za gehena

sizidzapambana motsutsa iwo,” vumbulutso lauzimu la Yemwe Iye ali.

<sup>33</sup> Zindikirani, “Ndipo Ine ndikuti iwe ndiwe Petro. Ndipo Ine ndidzapereka kwa iwe mafungulo aku Ufumu. Ndipo chirichonse chimene iwe uti umange pa dziko lapansi, ine ndidzachimanga icho Kumwamba; chirichonse chimene iwe uti uchimasule pa dziko lapansi, ine ndidzachimasula icho Kumwamba.” Tsopano, Iye amayenera kusunga Mawu Ake kapena Iye sanali Mulungu. Tsopano, ndipo pamene Iye anachita izo, masiku pang’ono kenako; Iye anapachikidwa, anawuka, anakwera kupita Kumwamba, ndipo Petro anatsegula Uthenga pa Tsiku la Pentekoste. Kodi iye anachita izo? Iye, ndithudi, iye anatero. Tsopano penyani, pamene iye akanati . . .

<sup>34</sup> Iwo onse anali akuwatonza iwo, chifukwa kuti iwo anali odzazidwa ndi Mzimu. Iwo ankatchedwa “osokonezeka, oyera-odzigidubuzwa,” kapena mtundu wina wa dzina monga choncho. Ndipo ngakhale kumaseka pa iwo, ndipo ankati, “Awa aledzera ndi vinyo watsopano.”

<sup>35</sup> Ndipo Petro atayimirira pakati pa iwo, anakweza liwu lake, ndipo iye anati, “Amuna ndi abale, mvetserani liwu langa. Mvetserani mawu anga ndipo mverani kwa ine. Awa sanaledzere monga inu mukuganizira kuti iwo ali; ili ndi ora lachitatu chabe la tsiku. Koma ichi ndi chiya chimene chinanenedwa ndi mneneri Yoweli, ‘Ndipo izo zidzachitika mu masiku otsiriza, kuti Ine ndidzatsanulira za mzimu Wanga.’ ndi chimene Iye akanati adzachite pa ana Ake aamuna, ndi ana Ake aakazi, ndi adzakazi Ake, ndi ena otero, mu tsikulo.”

<sup>36</sup> Ndipo pamene iwo anayamba kumvetsa izi, iwo anachekedwa mu mtima mwawo. Pakuti, iwo anamumva munthu yemwe sankadziwa ma ABC ake, komabe iwo amayenera kumvetsera kwa iye, podziwa kuti iye anali ndi Chinachake mkati mwa iye, chikumuwotcha iye mmenemo, Mzimu Woyera. Kumuletsa iye? Bwanji, izo zikanakhala ngati kuyesa kuti uzimitse moto, pa nyumba yowuma, pa tsiku la mphepo. Iwe sukanakhoza kuchita izo. Iye anali atadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo kodi iye anachita chiyani tsopano?

<sup>37</sup> Iwo anati, “Chabwino, amuna ndi abale, kodi ife tingakhoze kuchita chiyani kuti tipulumutsidwe?”

<sup>38</sup> Tsopano samalira, Petro, iwe uli nawo mafungulo aku Ufumu. Mwaona?

<sup>39</sup> Tsopano, pamene Yesu anawuka pa tsiku lachitatu, Iye analibe mafungulo aku Ufumu Wakumwamba. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Iye anati, “Ine ndiri nawo mafungulo a imfa ndi gehena,” koma osati aku Ufumu, chifukwa iwo anali atapatsidwa kwa Petro.

<sup>40</sup> Tsopano Iye anati, “Petro, chirichonse chimene iwe uti umasule pa dziko lapansi, Ine ndidzachimasula icho

Kumwamba. Chimene iwe umange pa dziko lapansi, Ine ndidzachimanga icho Kumwamba.”

<sup>41</sup> Tsopano apa iye akuyima ali ndi mafungulo, kuti atsegulire chinthu chodalitsidwa ichi kwa dziko. Ndipo apa iye ali nawo mafungulo mu dzanja lake. Ndipo iwo akumufunsa, “Kodi ife tingakhoze kuchita chiyani kuti tikhale opulumutsidwa?” Tsopano, ziribe kanthu chimene atumwi ananena kuti achite, Mulungu ayenera kuzindikira izo Kumwamba, ngati Iye anamupatsa iye ulamuliro umenewo.

<sup>42</sup> Tsopano Petro anati, “Lapani, wina aliyense wa inu, ndipo mukhale obatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Kodi uko ndi kulondola uko? Ndipo ndicho chifukwa mafungulo anatembenzika Kumwamba ku dzina lina lirilonse, njira ina iliyonse, ena a aliwonse—mawonekedwe ena aliwonse. Iwo anatembenzika pa dziko lapansi, ndipo iwo anatembenzika Kumwamba, kapena Yesu sanasunge Mawu Ake kwa Petro. Ndipo malo aliwonse mu Baibulo iwo anabatizidwa, pambuyo pa izo, iwo anali kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo iwo amene anabatizidwa izo zisanachitike, amayenera kubwera ndi kudzabatizidwanso kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti alandire Mzimu Woyera. Ndiko kukhoza. Izo zikuyendabe mofanana.

<sup>43</sup> Kotero, ngati ife tikuphunzitsa ubatizo mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” uwo ndi uneneri wabodza. Tsopano ine sindikufuna kuti ndikupwetekeni inu, koma ine ndiyenera kukanikizira izi pansi kotero kuti mpingo uwu udziwe chiyani. Ife sitiri pano ngati gulu la makoko ong’aluka losaphunzira; ife tikudziwa pamene ife tiri kuyima mu Mawu a Mulungu. Mwaona, ife tikudziwa. Ine ndikutsutsa wina aliyense kuti andisonyeze ine malo amodzi pamene wina aliyense anabatizidwapo konse mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Tsopano kodi inu mukamvetsera ku uneneri wabodza kapena Choonadi? Fufuzani Malemba. Izo ziri kwa inu.

<sup>44</sup> Ndiwonetseni ine pamene munthu mmodzi mu Baibulo, pamene mpingo unayamba wadzozedwa chipembedzo konse mu—mu Baibulo. Mundiwonetse ine mu Baibulo pamene iwo anayamba adzoza konse mlaliki wamkazi. Mundiwonetse ine mu Baibulo pamene zinthu zonse izi, zimene ife takhala tikuzikamba, zinayamba zadzozedwa konse mu Baibulo. Izo siziri mmenemo. Ndiwuzeni ine malo amodzi. Inu mumapita ku chipembedzo. . .

<sup>45</sup> Chabwino, pamene Amethodisti anawukapo, iwo ankalalikira kuyeretsedwa. Ndizo zabwino. Koma, pamene iwo anachita izo, iwo anapanga chipembedzo, ndipo icho



chinakhazikitsa izo. Ndicho chifukwa Baibulo linati, “Inu muli nalo dzina.”

Inu mukuti, “Ine ndine Mkhristu.”

“Chabwino, ndi chipembedzo chiti chimene inu muli ake?”

46 Inu mukuti, “Cha Methodisti,” bwanji, ndinu wachiwerewere ndiye. “Ine ndine wa Baptisti,” wachiwerewere. “Pentekoste,” ndinu wachiwerewere. Inu ndinu a mpingo umenewo.

47 Inu munayenera kukhala a Khristu. Mulibe ntchito yomanena kuti, “Methodisti,” “Baptisti.” Ngati ndinu Mkhristu, ndinu Mkhristu mu mtima.

48 Zirizonse za zipembedzo izo zikhoza kubala ana, ana a Mulungu, ndiko kulondola. Koma pamene inu muganiza kuti inu mukupita Kumwamba basi chifukwa chakuti ndinu wa Methodisti kapena wa Baptisti, inu mukulakwitsa. Ndipo ndicho chifukwa chimene ife tinakhala kunjira kwa chinthu chimenecho.

Chifukwa chiyani Abaptisti sangakhoze kuwona?

49 Ine ndinamufunsa munthu wa Methodisti kuno, akulemba lingaliro, limene analilemba kale lapita chabelo. Iye anati, “Chinthu chokha chimene ife tiri nacho motsutsa inu, inu mumapezeka pamene pali Achipentekoste.”

Ine ndinati, “‘Ifeyo’ ndi ndani?”

“Ife, Amethodisti.”

50 Ine ndinati, “Chabwino, ine ndikuuzani inu chimene ine nditi ndichite. Ine ndibwera ku mzinda wanu ndipo inu muwalole Amethodisti athandizire iwo.”

“O,” anati, “ndithudi, ife sitingakhoze kuchita izo.”

51 Ine ndinati, “Ndicho—ndicho chimene ine ndimaganza. Ine ndimakhala ndi Achipentekoste chifukwa Achipentekoste amakhulupirira izo. Ndiko kulondola. Iwo amasonkhanira pozungulira izo. Iwo ndi amene akupezapo phindu lake.”

52 Ndi angati amene anawerenga nkhanu ija mu *Life* magazini, posachedwa pomwepa, yokhudza mpingo wa Chipentekoste? Ndicho chimodzi cha zazikulu zopambana mu m’badwo uno. Iwo apeza otembenuka ambiri mu chaka chimodzi kuposa mipingo yina yonse kuyiyika pamodzi. Chifukwa chiyani? Ngakhale mwa zolakwitsa zawo, Mulungu ali kuwasunthira iwo patsogolo, chifukwa iwo anakhulupirira Choonadi ndipo akugubabe chamtsogolo ndi Icho. Ndi Choonadi.

53 Koma kodi ife tikuchita chiyani tsopano? Mwaona? Ndicho chifukwa ife sitiri chipembedzo. Ndipo motsimikiza basi monga Chipentekoste chikupanga chipembedzo. . .

54 Ndipo pamene mmbuyo kutali, pamene Mzimu Woyera unatsanuliridwa koyamba pa mpingo wa Chipentekoste, zaka makumi anai zapitazo, ndipo iwo nayamba kuyankhula ndi

malirime, imodzi ya mphatso. Ndiyo yochepesetsa ya mphatso. Ndiyo yakumapeto ya mphatso, malingana ndi Paulo Woyera, ndi kuyankhula ndi malirime. Ndipo mwamsanga momwe pamene iwo anawagwera, “O,” iwo akuti, “ife tawupeza Iwo tsopano,” ndipo iwo anapanga chipembedzo, General Council, chimene chiri tsopano Assemblies of God. “O, palibe amene ali nawo Iwo kupatula inu mutayankhula ndi malirime,” ndipo Mulungu anangosunthira kutali kumene kuchoka kwa iwo, ndi kuwasiya iwo atakhala pamenepo. Ndithudi. Inde, bwana.

<sup>55</sup> Motsatira kunadza Aumodzi, ndipo anaupenza uko ubatizo mu Dzina la Yesu. Iwo anati, “O, ife tiri nawo Iwo,” iwo anapanga bungwe. Kodi iwo anachita chiyani? Mulungu anangosunthira kunja komwe ndipo anawasiya iwo atakhala pamenepo.

Ndi za kwa, “Aliyense amene afuna, mumulole iye abwere.”

<sup>56</sup> Onani, Aumodzi sangakhoze kupita kwa Assemblies. A Assemblies sangakhoze kupita kwa Aumodzi. Ine ndayankhulapo kwa ena a amuna abwino amene iwo ali nawo, Bambo Goss, ndi Dr. Pope, ndi ambiri. Amuna amene ali amuna otchuka mu... Ine ndinakhala pansi ndi iwo. Ine ndinati, “Mungakhoze bwanji inu kuphunzitsa umboni woyamba umenewo, monga sikolala?”

<sup>57</sup> “Chabwino,” anati, “M’bale Branham,” mmodzi, awiri kapena atatu a iwo, anali owona kwenikweni, anati, “ife tikudziwa izo ndi zolakwika, koma ife tingakhoze kuchita chiyani? Ngati ife tinena chirichonse chokhudza izo tsopano, bwanji, icho chisokoneza dongosolo lonselo.” Zedi, ndipo inu simukhala bishopu pameneponso, woyang’anira wamkulu. Ndilo ganizolo.

<sup>58</sup> M’bale, ine kunalibwino ndikanakhala ndi mishoni yaying’ono pa ngodya, kapena kulalikira pansi pa mtengo wa paini, ndi kukhala nacho Choonadi, ndithudi, ndi kumadziwa kuti uli kunena Choonadi. Munthu amafuna Choonadi. Ndipo inu muli okakamizidwa, monga Mkhristu, kuti muzinyamula umboni wa Choonadi. Mulungu akakufunsani inu chifukwa cha izo.

<sup>59</sup> Ndiye, pa zinthu izi, ngati inu simunakhale mutabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo inu simunachite zinthu izi, ndipo inu simunalandire Mzimu Woyera . . .

<sup>60</sup> Inu mukuti, “O, ine ndinayankhula ndi malirime.” Izo sizikutanthauza kuti inu muli nawo Mzimu Woyera.

<sup>61</sup> Ine ndawonapo mfiti zachikazi, mfiti zachimuna, ziwanda, ndi china chirichonse, zikuyankhula mu malirime. Ndithudi. Iwo alibe ayi Mzimu Woyera, ndipo inu mukudziwa zimenezo. Kumwa magazi kuchokera mchigaza cha munthu, ndi kumavina, ndi kuyitana mdierekezi, ndi kuyankhula mu malirime. Ndithudi. Iwo alibe ayi Mzimu Woyera.

<sup>62</sup> Chotero, chifukwa inu mwayankhula ndi malirime, izo sizikutanthauza kuti inu muli nawo Iwo. Njira yokha imene inu mumadziwira kuti muli nawo Iwo, pamene mzimu wanu uchitirana umboni ndi Mzimu Wake, ndipo zipatso za Mzimu zikukutsatirani inu: chikondi, chikhulupiriro, chimwemwe, mtendere, kupirira, ubwino, kufatsa, ulemu. Ndi pamene inu mumadziwa kuti inu muli nawo Mzimu Woyera. Iwo umadzichitira umboni za Iwowokha.

<sup>63</sup> Tsopano, pamene inu mukuyesera kuti mudalire pa, chifukwa inu ndinu a Assemblies, kapena a Baptisti, kapena a Presbateria, inu mukuwona chimene inu mukuchita? Inu mukudzitengera dzina la wachiwerewere. Ndiko kulondola chimodzimodzi. Chokanimo mu chinthu chimenecho. Bweraniko muchoke kwa icho. Ine sindikutanthauza kutuluka mu mpingo wanu kapena chirichonse; inu muchite zimene inu mukufuna kuti muchite pa izo. Koma bweraniko muchoke podalira izo, “O, ine ndine wa Presbateria. Ife sitimakhulupirira mu masiku a zozizwitsa.” Chifukwa chiyani inu simukukhulupirira izo? Baibulo limaphunzitsa izo. “O, ine ndine wa mpingo wa Khristu. Iwo amanena kuti masiku a zozizwitsa anapita.” Iwo ndi aneneri abodza.

<sup>64</sup> Ine ndikhoza kukuwonetsani inu pamene Yesu Khristu anapereka Mphamvu kwa Mpingo, kuti ukachize odwala, ndi kuwukitsa akufa, ndi kutulutsa ziwanda. Ine ndikutsutsa munthu aliyense kuti andiwonetse ine Lemba mu Baibulo pamene Iye anazichotsa izo mu Mpingo. Ndi chiyani chimene chinatengera izo kutali? Mbalume yanu yomwe, kulondola, osati Mawu a Mulungu. Mzimu Woyera ukuchititsabe ntchitoyo kupangika, ukupitabe patsogolo pomwe chimodzimodzi basi, ndipo Iye adzatero kwa nthawizonse.

<sup>65</sup> Ndicho chifukwa ife sitiri chipembedzo ayi, “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, ndi kumakana Mphamvu yakeyo; kuchokera kwa oterowo tembenukirani kutali.” Ife sitimakhulupirira mu zinthu zimenezo.

<sup>66</sup> Tsopano, izo zinayambika motani konse? Ife tiyenera kufulumira ndi kufika kwa izo basi mwamsanga monga ife tingathere tsopano, momwe izo zinayambira konse. Tsopano ife tiri nawo Malemba ochuluka ndalemba apa okhudza Mzimu Woyera.

<sup>67</sup> Ndipo chinthu china, ife tinapanga kutsutsa usiku watha, pa “khama la oyera,” osati mwa njira imene Abaptisti amakhulupiririra izo. Ayi, bwana. Ine zedi ndimasiyana nawo Abaptisti ndi ganizo lawo, la kulingaliro kwawo kwa Chikalvini. Ine ndithudi sindimagwirizana nawo Apresbateria. Ine sindimagwirizana nawo Amethodisti pa njira yawo ya chiphunzitso cha Chiarmenia. Inde, bwana. Koma iwo onse ali nacho choonadi, koma iwe uyenera kuchibweretsa icho kumbuyo

*Kuno* kumene icho chiri Choonadi. Pamene inu muthamangira uko kunja, inu mumathamanga mopenga nazo izo. Ndithudi.

<sup>68</sup> Abaptisti anabwera mmenemo, anabatiza angapo kuno, mu kumiza; ndipo mlaliki anawabatiza iwo, asanu ndi anai pa khumi amasuta ndudu, kubwerera kunja ndi kukayima kunja uko, ndi kukasewera juga, matsenga usiku wonse, kuthamanga pozungulira, ndi malonda okhotakhota akatangale; ndipo akazi onse akuvala akabudula kunja kuno, akuthamanga konsekuno mu misewu, ndi kumadula tsitsi lawo, ndi—ndi kumasuta ndi kumayankhula, ndi maphwando aang’ono a kuluka-ndi-kusoka, ndi kumanena nthabwala zauve. Ndipo inu mukuchitcha chimenecho Chikristu? Ndipo inu mukuganiza kuti inu muli nacho chitetezero Chamuyaya? Inu mukupita ku Gehena monga choncho. Inu simukadzisangalatsira nokha Kumwamba mwa njira iliyonse. Ndithudi ayi. Chimenecho si chitetezero Chamuyaya.

Koma pamene munthu ali wobadwa kachiwiri wa Mzimu Woyera . . .

<sup>69</sup> Ndipo inu Apentekoste, chifukwa chakuti inu munadumpha mmwamba-ndi-pansi, munayankhula mumalirime, kuthamanga chokwera-ndi-chotsika mkampata, izo sizikutanthauza kuti inu muli nacho chitetezero Chamuyaya. Musati mutengere konse izo mmutu mwanu. Ayi, bwana. Izo ndithudi sizimatero. Chifukwa, inu mukudziwa kuti wanu womwe—moyo wanu womwe umakuchitirani inu, umboni, kuti inu simuli bwino ndi Mulungu. Ndiko kulondola. Inu simuli bwino. Chimenecho si chitetezero Chamuyaya, apobe.

<sup>70</sup> Koma ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake. Kodi chiripo chitetezero Chamuyaya? Baibulo linanena chomwecho. Baibulo linanena kuti maina athu anayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa dziko lisanayambe konse.

<sup>71</sup> Monga ine ndinanena mmawa uno, ine ndikunena izo kachiwiri. Munthu amene analemba nyimbo, “Panali dzina latsopano lalembedwa mu Ulemerero usikuuno, ndipo ndi langa,” lingaliro lake linali lonse labwino, koma iye anali kulakwitsa, Mwamalemba. Dzina lako silinayikidwe umo pa usiku umene iwe unapulumutsidwa.

<sup>72</sup> Dzina lako, malingana ndi Baibulo, malingana ndi Chivumbulutso 13, 17, ndi mwina motero, “linayikidwa pamenepo dziko lisanayambe konse; ndipo Yesu Khristu anaphedwa asanayikidwe maziko a dziko.”

<sup>73</sup> Mulungu akanakhoza bwanji, Yemwe ali wopandamalire; akanakhoza bwanji Mulungu wopandamalire, akudziwa mapeto kuchokera ku chiyambi, akanakhoza bwanji nkomwe Iye kuloleza tchimo kuti libwere pa dziko lapansi, ngati izo sizinali kwa cholinga?

74 Kungoti tiyikire kumbuyo tsopano zinthu zina zimene ife tazinena kale. Nchiyani chinali choyamba, Mpulumutsi kapena wochimwa? [Winawake mwa osonkhana akuti, “Mpulumutsi.”—Mkonzi.] Mpulumutsi, zedi. Ndi chiyani chimene chiri champhamvu kwambiri, Mpulumutsi kapena wochimwa? Ngati Mpulumutsi angakhoze kulichotsa tchimo, Iye ndi wamphamvu kwambiri. Chabwino, ndi chifukwa chiyani Iye analoleza tchimo kuti lichitike mu malo oyambirira? Kuti asonyeze kuti Iye anali Mpulumutsi. Nchiyani chimene chiri champhamvu kwambiri, mchiritsi kapena matenda? [“Mchiritsi.”] Mchiritsi. Ndiye nchifukwa chiyani Iye analola matenda kubwera? Kuti asonyeze kuti Iye anali mchiritsi. Ine ndikumverera mwachipembedzo pomwe pano. Inde, bwana. O, mai! Ndizo zikhumbo Zake.

75 Ndicho chifukwa Iye analola vuto kuti libwere. Ndicho chifukwa Iye analola chisoni kuti chibwere, kuti asonyeze kuti Iye ali chisangalalo. Zedi, izo ziri. Ndicho chifukwa ife tiri ndi usiku, kuti utsimikizire kuti ulipo usana. Ndicho chifukwa ife tiri nako kupsyamtima, kuti zisonyeze kuti ulipo mtendere. Zedi, ndi zotsutsa ndi zolondola. O, Iye ali wodabwitsa.

76 Tsopano, kodi izo zinayamba motani? Ife tifika molunjika kwa izo, basi mwamsanga monga momwe ife tingathere, kotero ine ndisakusungeni inu usiku wonse. Tsopano, apo payenera kukhala chiyambi cha zinthu zonse.

77 Ndipo ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu chinachake. Tsopano izi zikhoza... Inu mungoziyika izi mu thumba la chiburandi. Inu simusowa kuyika izi limodzi ndi mbale yozolowereka. Koma mvetserani kwa izi.

78 Ngati inu muli cholengedwa Chamuyaya, ndiye inu munalibe chiyambi konse, kapena simungakhale nawo mathero konse. Pakuti, *Muyaya* umachokera ku mawu a “chimene chiribe chiyambi kapena chiribe mapeto.”

79 Kodi inu simukukumbukira izo? Ine ndinanena, mmawa uno, kuti momwe Melkizedeki uja, pamene iye anakomana ndi Abrahamu akubwera kuchokera kokapha mafumu. Ndipo Baibulo linanena, mu Ahebri 7, kuti—kuti, “Levi anapereka zachikhumi kwa Melkizedeki, pamene iye anali mu chiuno cha abambo ake Abrahamu.” Abrahamu anabala Isaki; Isaki anabala Yakobo; Yakobo anabala Levi. Amenewo anali bambo, agogo aamuna, ndi agogo aamuna-a bambo ake. Ndipo pamene Levi anali mu chiuno cha agogo aamuna-a bambo ake, Baibulo likumupatsa iye kuyamikira chifukwa chopereka zachikhumi kwa Melkizedeki. Kuyankhula za Muyaya! Mai, mai! Iye sananene nkomwe kuti, “Iye anachita icho mwa mthunzi; iye mwakuyankhula kwina anachita izo.” Baibulo linati, “Iye anapereka zachikhumi.” Amen.

<sup>80</sup> Ndiye, ngati ife tabwera kupyolera mu mbewu yolondola, pamene Paulo analalikira Uthenga ine ndinali kumeneko ndipo inu munali kumeneko. Ife tifika poti tilowe mu zimenezo, mu miniti chabe, mpaka ku makutu athu. Zindikirani, ndicho chimene Lemba limadzinenera, kwa ife, ngakhale kupita kutali kumbuyo.

<sup>81</sup> Tangoganizani! Levi; kenako Yakobo, bambo ake; kenako Isaki, bambo ake; kenako Abrahamu, bambo ake; agogo aamuna a bambo ake. Pamene Levi anali mu chiuno cha agogo aamuna a bambo ake, iye anapereka zachikhumi kwa Melkizedeki.

<sup>82</sup> Ine ndikufuna ndikufunsemi inu. Awa anali ndani, Yobu 27...sate-eyiti, pamene Iye anati, “Iwe unali kuti pamene ine ndinkayika maziko a dziko lapansi? Pamene nyenyezi zammawa zinkayimba limodzi, ndipo ana aamuna a Mulungu anafuulira mwa chisangalalo?” Ana aamuna a Mulungu amenewo anali ndani amene anali kufuulira mwa chisangalalo? Yesu anawawuza iwo, kuti, “Ine ndinali nacho chisangalalo ndi inu maziko a dziko asanakhalepo.” Ife sitiri zolengedwa za nthawi. Ndife zolengedwa za Umuyaya.

<sup>83</sup> “Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine, kupatula Atate Anga atamukoka iye. Ndipo onse amene abwera kwa Ine, Ine ndidzawapatsa iwo Moyo Wamuyaya, ndi kumuwukitsa iye pa masiku otsiriza. Palibe mmodzi angakhoze kuwakhwathula iwo kuchokera mdzanja la Atate Anga, Amene akuwapereka iwo kwa Ine.” Inu mungataye motani?

<sup>84</sup> Onani, inu mukuchita mantha. Inu mukuwopa. Inu mukuthamanga mukuzungulira kuno. Ndipo ndiwo umodzi wa umboni wopambana, mu dziko, inu simunakhale muli kulikonse panobe. Ndiko kulondola. Mulungu angakhoze bwanji konse kukupulumutsani inu ngati Iye...

<sup>85</sup> Ndi angati mu mpingo uno mungakweze manja anu, ndipo mukukhulupirira kuti Mulungu ali wopandamalire? Inu mukudziwa chimene mawu oti *wopandamalire* amatanthauza? Ndizo zangwiro basi. Kupandamalire, inu simungakhoze—inu simungakhoze kuwafotokoza mawu oti *wopandamalire*.

<sup>86</sup> Kodi inu munayamba mwatengapo kamera yanu ndi kuyiyika iyo pa kupandamalire? Bwanji, izo zimangotanthauza kuchokera pamenepo kupitirira. Chabwino. Palibe njira yokujambulira iko mwina mulimonse.

<sup>87</sup> Chabwino, ndicho chimene Mulungu ali. Iye ali wopandamalire. Ndipo ngati Iye ali wopandamalire, apo sipakanakhoza kukhala pali nkhumbutera, popanda ntchentche, popanda tongole, popanda nsabwe, popanda thekenya, kapena popanda kanthu kamene kanayamba kakhalapo pa dziko lapansi, kapena kamene kakanati kadzakhalepo konse, koma kamene Mulungu anakadziwa iko dziko lisanawumbidwe konse. Apo pali lingaliro lina la kupandamalire.

<sup>88</sup> Chabwino, ndiye, Mulungu wopandamalire Amene amakupulumutsani inu pano, akudziwa kuti Iye akuti adzakutayeni inu sabata lotsatira, kapena mwezi wamawa, kapena chaka chamawa, bwanji, Iye akugonjetsa cholinga chomwecho. Iye sangakhoze kukutayani inu. “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha ndipo sadzabwera konse mu Chiweruzo, koma wadutsa kale kuchoka ku imfa kupita ku Moyo.” Sangakhoze kuchita izo. Inu sibwezi mutatinso. . .

<sup>89</sup> “Iye amene ali wobadwa wa Mulungu samachita tchimo; pakuti mbewu ya Mulungu imakhala ilipobe mwa iye, ndipo iye sangakhoze kuchimwa.” Iye angakhoze bwanji kuchimwa pamene apo pali nsembe ya tchimo kwa iye?

<sup>90</sup> Ine ndingakhale bwanji wodwala pamene ine ndiri mu thanzi langwiwo? Ine ndingakhoze bwanji kukhala wakhungu pamene ine ndikukhoza kupenya? O, mai! Ine ndingakhoze bwanji kukhala mnyumba ndi kunja kwa nyumba pa nthawi yomweyo? Ine ndingakhoze bwanji kukhala woledzera ndi wosaledzera pa nthawi yomweyo? Iwe sungakhoze kuchita izo.

<sup>91</sup> Ndipo pamene iwe wapulumutsidwa, iwe uli pansu pa Chitetezero, ndipo machimo ako sawerengedwa kwa iwe. Kodi Davide sananene kuti, “Wodala ali munthu yemwe Mulungu sadzamuwerengera ayi tchimo, ndi kuyika tchimo kwa iye?” Mulungu samasunga tchimo motsutsa cholengedwa Chake. Ndizo zamphamvu. Umenewo si mkaka wa mmaere. Koma ndilo Baibulo. Mulungu sadzawerengera tchimo kwa wolungama.

<sup>92</sup> “Mulungu,” mwa chisomo Chake, kupyolera mu kukonzedweratu, “osalolera kuti aliyense awonongeke konse, koma kuti onse akhoze kubwera ku kulapa.” Koma pokhala wopandamalire, ndi podziwa yemwe akanati adzabwere ndi yemwe sakanati adzabwere, Iye akanakhoza kukonzeratu chirichonse kuti chigwire ntchito kwa chifuniro Chake. Ngati Iye akanati asachite izo, nchifukwa chiyani Iye analoleza tchimo mu malo oyambirira? Pamene Iye anali Mpulumutsi. . . Ngati pakanakhala kuti panalibe wochimwa, Iye sakanakhala konse Mpulumutsi; chikhumbo, chimene chinali mwa Iye, sichikanakhoza kusololedwera kunja.

<sup>93</sup> Iye anadzakhala motani mchiritsi konse? Iye anadzakhala motani mchiritsi konse? Chifukwa Iye analoleza matenda kuti abwere, kuti Iye akakhoze kudziwonetsera Iyeyekha ali mchiritsi. Iye anali mchiritsi. Inu mukanakhala motani konse. . . Iye akanadziwika motani konse? Chikhumbo Chake chikanakhoza kugwira motani ntchito konse? Iye akanakhoza motani kukhala mchiritsi konse, ngati pakanakhala palibe konse matenda alionse? Iye anayenera kuti aloleze matenda.

<sup>94</sup> Nzosadabwitsa, Paulo anati, mu Aroma 8. “Munthu wopusa, ndi ndani yemwe angamuuze—wowumba choti achite nalo

ilo; ndani, pamene dongo linawuka ndi kunena, ‘Bwanji mukundipanga, inu, ine motere?’ Kodi Iye sanawutse Farao kwa cholinga chomwecho, kuti Iye akakhoze kusonyeza ulemerero Wake uko ku Igupto? Iye amalimbitsa yemwe Iye amufuna, ndi kumulungamitsa yemwe Iye amufuna. Si iye amene afuna, kapena iye amene athamanga, koma Mulungu amene amawonetsa chifundo.

<sup>95</sup> Koteru, inu munalibe kanthu kochita nazo izo. Inu mulibe chinthu chimodzi choti muchite. Ngati chiri chisomo, ngati iyo ili mphatso yaulere, apo palibe chinthu chimene inu mungakhoze kuchita za iyo. Mulungu wayipereka iyo kwa inu, ndipo ndicho chifuniro cha Mulungu. Ndicho chinthu chimene Mulungu wakonzera kwa inu.

<sup>96</sup> Baibulo linanena kuti ife “tinakonzedweratu kudzakhala ana okhazikitsidwa, ana a amuna a Mulungu, asanakhalepo maziko a dziko.” Ndiye, pamene Mulungu anapha Mwanawankhosa, mu kuganiza Kwake Komwe, asanakhalepo maziko a dziko, kuti atsimikizire zikhumbo Zake, chimene Iye anali; pamene Mwanawankhosa anaphedwa, ife tinaphedwa palimodzi ndi Iye. Pamene Magazi a Mwanawankhosa anagwidwa mu malingaliro Ake Omwe, kumbuyo uko asanayikidwe maziko a dziko, maina anga ndi anu analembedwa pa Bukhu pamenepo, zonse mu kuganiza Kwake kwakukulu.

<sup>97</sup> Iye ali wopandalire. Ngati Iye sanatero, chifukwa chiani Iye analoleza izo? Champhamvu kwambiri ndi chiti, ine ndati, Mpulumutsi kapena wochimwa? Ndi chiti chimene chiri ndi mphamvu zambiri? Ndiye, champhamvucho chinayenera kuloleza chofookeracho, ndipo Iye amangochita izo kwa ulemerero Wake. Pamene Iye anamupanga Lucifara, Iye ankadziwa kuti iye akanadzakhala mdierekezi. Iye amayenera kuloleza kuti izo zikhale pamenepo kuti akasonyeze kuti Iye anali Mpulumutsi, Khristu. Iye amayenera kuloleza izo kuti zichitike mwa njira imeneyo.

<sup>98</sup> Tsopano, kodi Baibulo silimanena, kuti, “Zinthu zonse zimagwirira ntchito limodzi kwa ubwino wa iwo amene akonda Mulungu”? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Koteru inu mukuchita mantha ndi chiyani?

Tiyeni ife tikhale chiriri ndi kumachita,  
 Ndi mtima chifukwa cha ndewu iliyonse.  
 Tisakhale ngati ng’ombe yoyendetsedwa  
 yosayankhula, kukhala woti achite  
 kupemphedwa ndi kunyengereredwa!  
 Ndi kukhala wolimbamtima!

<sup>99</sup> Ine ndimakonda zimenezo. Kuyimirira njo! Ndakatulo yaying’ono imene inkandithandiza ine mochuluka kwambiri pamene ine ndinali mwana, imamveka chinachake monga chonchi.



Kunali Wachiroma wolemekezeka,  
 Mu masiku a Mfumu ya Chiroma;  
 Yemwe anamumva wamantha akufuula,  
 Pamaso pa linga akuti:  
 “O, ndi motetezeka mu mtengo wa mkuyu  
 woterowo,  
 Palibe mmodzi yemwe angakhoze  
 kuwugwedeza iwo.”  
 “O, ayi,” anatero wolimbantimayo,  
 “Ine ndipeza njira kapena kuwuchitisa iwo.”

<sup>100</sup> Ndi zimenezotu. Ndiko kulondola. Ngati Baibulo ili limaphunzitsa kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. . . Icho sichinali chinthu chophweka pamene ine ndinatuluka mu kachisi muno tsiku lija, ndipo aliyense akundiuzwa ine kuti *izi* zikanachitika, ndipo *izo* zikanachitika. “Iwe ukanatengedwa ngati wotentheka, kuponyedwa mu ndende, ndipo gulu lonse la azamankhwala likanakhala likukutsutsa iwe.” Koma Mulungu anati chita izo. Baibulo linati Iye anali. Ndipo tsopano moto wa chitsitsimutso ukuyaka mu fuko lirilonse pansu pa Kumwamba. Bwanji? Kuimirira kwa icho!

Kodi inu mumayichita bwanji ntchito yanu tsiku lirilonse?  
 Kodi inu mukuwopsyedwa nayo ntchito imene inu mwayipeza?  
 Kodi inu mungakhoze kuyima chiriri ku ntchito ili mtsogolo?  
 Kodi inu muli otopa ndi malingaliro opandakanthu? (ine ndimadana nazo zinthu zimenezo.)  
 Kapena kodi inu mumayima kumene mpaka ku ntchito ili mtsogoloyo,  
 Kapena kodi mantha akuthamanga popyola mu iyo yonse?  
 Ngati choncho, chitani yotsatira imene inu mutayipeze,  
 Pa kuganiza kuti inu mukupita kuti mukayichite iyo.

<sup>101</sup> Mukhale nayo iyo. Ndithudi. Lingani mu mtima mwanu, monga Daniele. Khalani ndi Mulungu.

<sup>102</sup> “Kodi izi zonse zinachitika kuti? Izo zinachitika motani? Nchiyani chimawapangitsa anthu kutero? Nchifukwa chiyani ife tangotsala pang’ono kuti tiwonongedwe? M’bale Branham, fotokozani kwa ine. Ndi chiyani chimene chimakupangitsani inu kuganiza kuti chinthu chonse ichi chiyenera kuti chifafanizidwepo?” Icho chinafafanizidwapo kamodzi kale, (ndi kulondola uko?) mu chiwonongeko cha chigumula. Tsopano

apa pakubwera zinthu zakuya zina. Ndipo ife tikonzekera kuti tiwerenge.

<sup>103</sup> Tsopano ine ndikufuna inu mutembenuze ndi ine tsopano, uko mu Bukhu la Genesis, pa mutu wa 3. Ngati inu mukufuna kuti mudziwe chirichonse, ine ndikhoza kukuwonetsani inu mu Bukhu ili la Genesis pamene mwambo uliwonse ndi lingaliro lililonse, ndi chirichonse chimene ife tiri nacho lero lomwe, chinayambira mu Genesis. Ndi angati amadziwa kuti *Genesis* amatanthauza “chiyambi”? Ndithudi.

<sup>104</sup> Ife tikuwupeza mpingo wa Katolika mu chiyambi, Babeloni, Nimrodi woyambitsa; ife tikuwupeza iwo pakati pa Baibulo, ife tikuwupeza iwo kotsiriza kwa Baibulo; ife tikupeza, akuyesera kubweretsamo alaliki aakazi, mu chiyambi cha Baibulo, pa kupembedza zoyimikidwa zazing’ono zopangidwa kuchokera ku mizu. Ndi angati amene anayamba awerengapo za Hislop, *Two Babylons*, mbiriyakale? Chabwino. Kafufuzeni, mu mbirizakale izi. Iwo anali ndi mkazi... Ndiyeno inu mukukumbukira, ngakhale Yakobo anaba timulungu ta abambo ake, ndipo mwana wake wamkazi anatibisa ito pansi pake ndi kutitengera ito kunja uko mu chipululu, timene tinayipitsa msasa, kenako. Chabwino.

<sup>105</sup> Tiyeni tiwerenge apa tsopano mu Genesis.

*Tsopano serpenti anali wochenjera kwambiri kuposa chinyama chirichonse cha kuthengo chimene AMBUYE Mulungu anali atachipanga. Ndipo iye ananena kwa mkaziyo, Eya, anati Mulungu kuti, Inu simudzadya za mtengo uliwonse wa mmunda?*

*. . .mkaziyo ananena kwa serpenti, Ife tikhoza kudya za chipatso cha mitengo ya mmunda:*

*Koma za chipatso cha mtengo . . .mkati mwa munda, Mulungu wanena kuti, Inu musadye za icho, ngakhale inu kuchikhudza icho, kuwopa kuti inu mungafe.*

*Ndipo serpenti ananena kwa mkaziyo, Inu sikuti mudzafa ndithu :*

*Pakuti Mulungu akudziwa kuti mu tsiku limene inu muti mudzadye za icho, ndiye maso anu adzakhala otseguka, (mukuona, kusaka Kuwala kwatsopano), ndipo inu mudzakhala monga milungu, odziwa chabwino ndi choyipa.*

<sup>106</sup> Mukuona momwe anthu awa aliri lero, kuyesera kuti azichotserapo mu Baibulo? “Bwanji, kodi izo siziri mophweka mofanana basi kutsanulira, kapena kukonkha, kapena njira *iyi*, kapena njira *iyoyi*?” Ayi, bwana. Mulungu anayalika dongosolo, ndipo ndiyo imene ife tiyenera kuti tizitsatira, *Iyi*. [M’bale Branham akuloza Baibulo lake—Mkonzi.]

*Ndipo pamene mkaziyo anawona kuti mtengowo unali wabwino kukhala chakudya, ndipo kuti iwo unali*

*wosangalatsa kwa maso, ndi mtengo kuti upange. . .  
kuti uzikhumbiridwa kuti umupangitse wina nzeru,  
iye anatenga za zipatso zake, ndipo anazidya, ndipo  
anakaperekanso kwa mwamuna wake limodzi naye;  
ndipo iye anazidya.*

*Ndipo maso awo a iwo onse anali otseguka, ndipo  
iwo anadziwa. . .iwo anali amaliseche; ndipo iwo  
anadzisokera masamba a mkuyu limodzi, ndipo  
anadzipingira okha matewera.*

<sup>107</sup> Ine ndikanakonda kuti ndiyime apa kwa miniti. Tsopano, payenera kuti pakhale chiyambi cha chirichonse. Inu munali nacho chiyambi. Tsopano ife. . .Apa ndi pamene ine ndikufuna kukhazikitsirapo chinthu chonsechi pamenepa, tsopano, ife takamba za izo mu misonkhano iwiri yotsiriza iyi, ndi mpaka apa.

<sup>108</sup> Tsopano, mmawa uno ife tinapita kumbuyo ndipo tinachita mwasewero, ku Baibulo, kuti pamene Mulungu anali kupanga dziko lapansi, kuti pamene Iye anali kupanga mipweya; ndiyeno mipweya imeneyo inadzakhalala kashiamu, ndi potashi, ndi—ndi zinthu zosiyana. Iye anali akupanga thupi lanu. Iye anali akuyala nyumbayo, monga mmisiri wamkulu wodziwa, monga womanga akuyalika zida zake kuti amange ntchito ya manyumba. Iye anali akupanga thupi lanu, ndipo Iye anali nalo ilo liri pamenepo. Iye ankadziwa chimodzimodzi basi, mu malingaliro Ake, chimene chinali choti chichitidwe.

<sup>109</sup> Dzanja ili, Mulungu anapanga dzanja limenelo Iye asanati. . .pamene Iye anali akupanga dziko; koma, mzimu wanga Iye anawupanga pasanakhale dziko. Tsopano, koma dzanja ili ndi thupi ili, Iye anazipanga pamene Iye ankapanga dziko, chifukwa thupi ili linabwera kuchokera ku dziko lapansi, ndipo likubwerera ku dziko lomwe. Mulungu anazipanga izo. Iye anaziyika izo zonse kunjira mu choyang'anirapo Chake chachikulu ndi dongosolo Lake.

<sup>110</sup> Tsopano, pamene Iye anapita koti apange dziko lapansi, Iye anamupanga munthu, ndipo munthuyo sankawoneka bwino kumene. Tsopano ife tinali nazo izo, mmawa uno, tinapita kupyola mu sewerero, momwe kuti—Atate anabwera pansu ndipo anayang'ana pa mwana Wawo, wopangidwa mumawonekedwe Awo, ndi zina zotero. Ndiye Iye anamupangira iye mkazi, mzake womuthandizira.

<sup>111</sup> Tsopano, kumbukirani, kuti, zonse za zolongedwa za dziko lapansi, Adamu anali atazitcha izo maina.

<sup>112</sup> Iye anapanga—ng'ombe, ndi zamoyo, ndi chirichonse. Ndipo lero, ife. . .Olondoza zaka ndi—ndi malingaliro osiyana aakulu a sayansi, akhala akuyesa, kwa zaka zikwi zisanu ndi chimodzi, kuti achipeze chilumikizo chosowa chimenecho, chifukwa

chache nyama imeneyo...Munthu ali moyo wanyama. Ife tikudziwa zimenezo, kuti ife tapangidwa . . .

113 Ndipo mkazi ali chabe gawo la mwamuna, chochokera ku china. Mkazi sanali mu kulenga koyambirira. Mulungu anali atasiya kulenga, kwa zaka ndi zaka ndi zaka, mpaka Iye anamupanga mkazi kuchokera mu nthiti ya mmbali yake. Adamu anali atatchula maina kale chirengedwe chonse, china chirichonse, koma iye sanali kanthu kwa iyemwini. Koteru, Iye anamupangira iye mzake womuthandizira; anatenga nthiti kuchokera mu mbali yake, anatseka potsegukapo, ndipo anapanga mzake wothandizira kwa iye. Ndipo mwamuna, mwa mzimu wake, anali zonse mwamuna ndi mkazi.

114 Ndipo mkazi ali chabe gawo la mwamuna. Ndipo pamene mwamuna adzitengera kwa iyeyekha mkazi, ndipo ngati iye ali molondola mkazi wake, mkazi-wopatsidwa ndi Mulungu, iye adzakhala basi kwa iye ngati gawo la iye.

115 Ndicho chifukwa inu muli ndi zosokonezeka zambiri mu ukwati, ndi chifukwa chakuti inu mumapita panja ndi kukawona msungwana wina wa maso okongola abulauni kapena maso a buluu, kapena chinachake monga icho, ndi mawonekedwe ena okongola, ndipo inu mumamugwera iye. Nthawi yoyamba yomwe iye ati akhale ndi mwana wake woyamba, mano amenewo amagweruka, ndipo iye amayamba makwinya ndi kukalamba, ndiye inu mumafuna kumukankhira iye kunja. Ndipo ena a inu akazi mumapeza mnyamata wina wamng'ono wa tsitsi lonyololekera pansu, ndipo chitini cha mafuta cha amayi ake chitakhuthulidwira mwatheka pa ilo, ndipo litapoteka. Ndipo ilo lonse lidzakuzukamo; ine ndikudziwa izo mwa zondichitikira. Koma ndi chiyani chimachitika? Ndi chiyani icho? Inu munagwera pa zimenezo.

116 Inu mumayenera kuti mupemphere, poyamba, chifukwa mkazi ali gawo la inu. Ndipo ngati inu mwamukumbatira mkazi mu chifuwa chanu, ndi kumutenga iye kukhala mkazi wanu, ndipo inu . . .Iye amapanga chidindo pa inu. Ife tinena izo monga chonchi kuti inu mumvetse. Ndipo mkazi wina aliyense akabwera pa chifuwa chimenecho sakwanira chidindo chimenecho. Ndipo Mulungu adzakufunsani inu chifukwa cha izo. Ndipo inu musingokumbukira zimenezo.

117 Inu amene mumatenga mkazi wa winawake ndi . . .Ine ndinamva lero za msungwana wamng'ono kuno mtawoni, kanthu kakang'ono kosawuka. Ine ndikumudziwa iye. Ndipo wa juga wina akumugulira iye zovala zina zabwino zazikulu, ndi zinthu, ndi kuyesera kuti azisewera kwa iye monga choncho. Khoswe, angati achite chinthu monga icho, sangati ngakhale kuti azilingaliridwa ngati munthu.

118 Inu mukudziwa, garu sali motsika-pansu chotero, ndipo komabe inu mumamutcha mayi wa garu "slut." Iye ali nawo

makhalidwe ochuluka kuposa theka la akazi aku Jeffersonville ali nawo. Ndipo inu mumamutcha mayi wa nkhumba “sow,” ndipo iye sali ayi. . . Iye ali mochuluka wakhalidwe kuposa akazi a United States uyu, ambiri a iwo. Ndiko kulondola chimodzimodzi. Tsopano, ine ndikudziwa kuti ndizo zomveka. Ndipo ine ndinakuwuzani inu kuti ine ndiperera izo pachimake, ndipo ine ndikufuna inu kuti mudziwe zimenezo. Ndipo ndizo zoono. Iwo onse, akazi masiku ano, sadziwa nkomwe chomwe khalidwe liri. Anati, “Siziri kupweteketsa chikumbumtima changa.” Chabwino, iwe ulibe chirichonse. Zindikirani. Inde, bwana. Pamene, iwe ukudziwa chimene chiri cholondola ndi cholakwika.

119 Tsopano zindikirani. Munthu uyu, pamene iye analengedwa, Mulungu analekanitsa mzimu wake. Ndipo Iye anatenga chidutswa kuchoka kwa mwamuna, mbali yake, ndipo anapanga mkazi kuchokera kwa icho. Ndiyeno Iye anatenga waukazi, mzimu wokongola wa mwamuna, ndipo anapanga mkazi kuchokera kwa iwo. Ndipo Iye anamupanga mwamuna, wamphongo, wanyonga.

120 Ndipo pamene inu mumuwona m—m—mwamuna yemwe ali wamng’ono. . . inu mukudziwa, akuzilocha, kapena chirichonse chimene inu mumachitcha icho, zikhadabo zake; ndipo, inu mukudziwa, zinai pa mbali imodzi ndi zisanu pa inayo, ndi—ndi kunyololetsa tsitsi lake chammunsi; ndi kunyamula kamwa yake ili yotseguka kutsogolo, ndi chinthu chotero monga icho; ena a anyamata okongola awa. Inu mungokumbukira, mlongo, pali chinachake cholakwika ndi mbalame imeneyo. Pali chinachake cholakwika. Kulibwino muyike diso lanu pa iye.

121 Ndipo pamene inu mumuwona mkazi ali ndi ndudu pambali pa kamwa yake, atavala maovololo, ndi kumanena kuti, “Ine ndikuuza iwe, mnyamata, chimene icho chiri!” M’bale, inu mumuyang’ane msungwana wokalamba uyo. Apo pali chinachake chalakwika ndi iye.

122 Mkazi, akuyenera kuti akhale mkazi, ndipo iye akuyenera kuti azivala monga mkazi. Pamene Mulungu anamupanga mwamuna, Iye anamupanga iye chinthu chimodzi; ndipo Iye anamupanga mkazi chinthu chinachakenso. Ndipo pamene Mulungu amumveka mwamuna, Iye anamumveka iye njira yina, ndipo mkazi chinachakenso. Ndipo Baibulo linati, “Ndi themberero kuti mkazi azivala chovala chimene chiri choyenera kwa mwamuna.

123 Ndipo akazi inu, mumavala mathalauza aang’ono akale awa ndi zinthu, ndi kumazivala izo kunja kuno, zazing’ono zakale. . . Nchiyani chimene inu mumazitcha izo, bokati? Kodi iwo amazitcha chiyani izo? . . .? . . . Ayi, ayi, si akabudula. Ndi zimene ziri ndi miyendo yayitali kwa izo. [“Zokankhira

maphedulo.”] Zokankhira maphedulo, ndi maovololo, mandakoka.

Kulowa mkati, ndi kunena, “Izi ndi za madona.”

<sup>124</sup> Ine ndinati, “Ayi, inu mwalakwitsa. Madona samavala zinthu zimenezo. Akazi akhoza, koma madona savala.” Ndiko kulondola.

<sup>125</sup> Baibulo linati, “Ndi themberero kwa mkazi kuti avale chovala; ndi kwa mwamuna kuti avale chovala chimene chiri choyenera kwa mkazi.”

<sup>126</sup> Ndipo mwamuna akukhala wachikazi mochulukira, tsiku lililonse, ndipo akazi akukhala aumphongo mochulukira. Chavuta ndi chiyani? Ife tizipeza izo mu maminiti ochepa, mwa Baibulo. Akazi sali akazi panonso. Ine sindikutanthauza inu akazi Achikhristu. Inu ndikuyankhula za ena wamba. Iwo akufuna kumachita ngati mwamuna; akufuna kuti azidula tsitsi lawo ngati mwamuna; kuyika dzanja lawo pamwamba pa chigwiriro, monga *choncho*, ndi kumayimba *Mulungu Dalitsani Amereka*, ali ndi ndudu pa ngodya ya kamwa yawo.

<sup>127</sup> Kupita uko pa msewu, nsana poyera monga *choncho*, ndipo mu msewuwawukulu umene. Ife tinawawerenga. . . Ine ndikufuna ndikuwuzeni inu chinachake. Ndipo inu madalaivala aakazi, mvetserani. Billy Paul ndi ine, pa msonkhano wotsiriza uwu kuzungulira fuko, miyezi khumi ndi umodzi, ine ndinasunga chiwerengero cha ziphapha pa msewu. Ndipo mwa zolakwika mazana atatu, pa msewu, mulote ndi zingati za izo zinali madalaivala aakazi? Apo panali kusowa chabe. . . Khumi ndi asanu ndi anai anali amuna. Ndipo mazana awiri ndi makumi asanu ndi atatu kapena, ine ndikukhulupirira iwo anali, mazana awiri ndi makumi asanu ndi atatu mphambu mmodzi ndiye akanati akhale madalaivala aakazi. Madalaivala aakazi! Tsopano, ine sindikunena kuti palibe madalaivala abwino aakazi. Koma iye akhoza kutembenukira mbali iliyonse.

<sup>128</sup> Ndipo inu mungoyesa kubwerera mmbuyo kwa iye? Kumulola iye kukhala ngati wa mawonekedwe abwino, ayima pamenepo, akukankhira tsitsi lake mmwamba pamene msilikali akubwera pamenepo. “Bwanji,” iye anena kuti, “ndithu, inu ndinu wolakwa!” Ife tiribe lamulo.

<sup>129</sup> Iwo anatsimikizira izo tsiku lina mu mulandu wa msonkho umene ine ndangodutsamo kumene. Ife tiribe malamulo ayi. Ngati alipo. . .

<sup>130</sup> Nzosadabwitsa mabwana aakulu aku England anati, “Demokarase inali yonse bwato lopanda nangula.” Ndiko kulondola, kuyima pa bokosi la sopo, kumachita zamasankho. Demokarase ndi yovunda, choteronso olamuliramwaukali ndi onse ena a iwo. Chinthu chonsecho ndi chovunda. Palibe koma chinthu chimodzi choti Mulungu achichite, ndicho kuwononga chinthu chonsecho, monga Iye ananena kuti Iye akanadzachita,

ndi kuyamba mwatsopano. Tsopano penyani kuyandikira kwache momwe ife tiriri ku Kudza.

<sup>131</sup> Tsopano pamene mkazi uyu...Iye anamupangira iye mzake womuthandizira, ndipo iye anati woti akhale mzake womuthandizira. Ndiyeno. . .

<sup>132</sup> Tsopano, pano, ine sindinayambe ndakhala naye mlaliki woti agwirizane nazo izi panobe. Ndipo iwo amayesera kuti azipange izo njira yinayake, komabe izo sizipanga zomveka kwa ine. Iwo amayesera kunena kuti Adamu ndi Eva anadya maapulo ena ake. M'bale, ngati. . .ine sindikunena izi mochita nthabwala tsopano, koma ine ndikufuna kunena icho. Pakuti, ngati kudya maapulo zimawapanga akazi kuzindikira kuti iwo ali maliseche, kulibwino ife tipereke maapulo kachiwiri. Ndipo inu mukudziwa kuti ndiko kulondola.

<sup>133</sup> Inu mukudziwa, kuti kudya apulo, icho sichinali chimene iwo anachita, chinawapanga iwo kuzindikira kuti iwo anali amaliseche. Ndithudi, icho sichinali. Icho chinayenera kubwera uko mwakugonana. Icho chinayenera kuti chikhale, chifukwa iwo anazindikira kuti iwo anali amaliseche pamene iwo anatenga chipatso choletsedwa ichi. Kodi mkazi sali mtengo wa chipatso? Kodi inu simuli chipatso cha amayi anu? Chipatso chake chinali chimenecho chimene chinali kuletsedwa kuti chikhale chikutengedwa.

<sup>134</sup> Tsopano apa pali chinthu chachikulu. Tsopano chapafupifupi chimene sayansi inayamba yakhala nacho kuti adziwe chimene munthu wokhalapo anali. . .Iwo amakumba mafupa akale, iwo amatenga ziwalo zokumbidwa, ndipo iwo amatenga mitu, ndipo iwo amatenga zigaza, ndi mikono, ndi mafupa, ndi kuyesa kuzipanga izo kuwoneka ngati munthu wokhalapo. Ndipo iwo akudziwa kuti chinthu chapafupi kwambiri chimene iwo anachipeza konse kwa munthu, choyandikira kwa iye, ndi chimpanzi. Iye ali mtundu wapafupi kwa munthu wokhalapo; komabe icho sichiri kanthu ndi munthu wokhalapo, wapamwamba kwambiri.

<sup>135</sup> Mawonekedwe otsikitsitsa a moyo amene alipo ndi chule; mawonekedwe apamwamba kwambiri ndi munthu wokhalapo. Mulungu anayambira pansu ndipo anapanga chokwera kumene, mpaka Iye anabweretsa izo mpaka ku chifaniziro Chake. Anazibweretsa izo kupyolera ku mbalame ndi zirombo, ndi kupitirira mmwamba, mpaka Iye anafika ku chifaniziro cha Mulungu. Iye anamupanga munthu mu chifaniziro chimenecho. Ndiwo mawonekedwe apamwamba kwambiri. Mawonekedwe otsikitsitsa ndi mbululu chabe imene inasandulika kukhala chule ndi zina zotero.

<sup>136</sup> Tsopano, chilumikizo chosowa ichi, chimene iwo sakukhoza kuchipeza. Penyani Lemba tsopano. Inu, inu simugwirizana nazo izi, ambiri a inu, koma ine ndikufuna. . . ndikungofuna inu

muzisunge izi mumalingaliro. Ndipo musati mukondere potsutsa izi. Mvetserani.

<sup>137</sup> Ine ndikudziwa kuti ambiri a inu mwakhala mukumvetsera posachedwapa kwa Dr. DeHaan. Ine ndithudi . . . Ngati munthu wa udindo wakewo, ndi m'bale wabwino wa Chibaptisti, ndipo ine ndithudi ndikumuyamikira iye. Iye ali nalo luntha lochuluka ndi ubongo, ndipo—ndipo ndayiwa zoposa momwe ine ndikanadziwira konse; chifukwa iye ndi Dokotala wa—wa Zauzimu, ndipo iye ndi dokotala wazamankhwala, ndipo iye ndi Dokotala wa Sayansi. Iye ndi munthu wanzeru. Koma iye akunena kuti iwo. . . Pamene ana aamuna a Mulungu anawawona ana aakazi a wanthu kuti anali okongola; iye amatenga mayimidwe a Josephus, ndi kunena kuti “iwo—iwo anadzikanikizira okha mu thupi la umunthu,” ndi kudzitengera kwa iwo akazi. Ndipo uko kunali zimphona mu dziko la Nodi. “Ndipo iwo anadzitengera okha akazi ndi kukhala nawo iwo, pamene ana aamuna a Mulungu, Angelo akugwa, anatenga ndi kuwawona ana aakazi a wanthu; ndipo chikhumbo cha kugonana chinali chinthu chachikulu motero, ndipo komabe iwo pokhala ochimwa muja anagwa, iwo anadzikanikizira okha kulowa mu thupi la umunthu.”

<sup>138</sup> Ngati iwo akanachita izo, iwo akanawononga machiritso Auzimu, iwo akanawononga china chirichonse. Ngati mdierekezi angakhoze kulenga, iye ali wofanana ndi Mulungu. Mdierekezi sangakhoze kulenga. Ine ndikufuna inu mundisonyeze ine malo amodzi pamene mdierekezi angakhoze kulenga. Iye sangakhoze kulenga ayi. Iye amangosokoneza chimene chalengedwa. Iye sali mlengi. Iye ali kokha wosokoneza.

<sup>139</sup> Chabwino, ndiye, nchiyani chinachitika? Penyani. Pano pali kufotokoza kwanga. Pano pali chilumikizo chosowacho.

<sup>140</sup> Tsopano iwo ali ndi chimpanzi, koma inu simungakhoze kugonanitsa chimpanzi ndi mkazi ndi kubalapo mwana. Inu simungakhoze kugonanitsa munthu ndi chinyama chirichonse. Izo sizingasakanizikane. Inu simungakhoze kuchipatsa magari, chinyama chirichonse.

<sup>141</sup> Pamene ine ndinali mu Afrika, iwo ankachita nawo anthu osawuka achikuda awo kumeneko mwa njira yoteroyo; winawake ananena kwa ine, anati, “Iwo sali kanthu koma zinyama.”

<sup>142</sup> Ine ndinati, “Ine ndikupempha kukhululukira kwanu. Iwo ali basi mochulukira munthu monga inu muli, mwinamwake mochulukira pang'ono.” Ndiroleni ine ndikuwuzeni inu, pamene inu mukhala ndi kulinga kwa mtundu umenewo, inu mukubwerera mmbuyo cha kwa chinyama. Ine ndinati, “Munthu ameneyo, ngati iye ali wakuda monga chitsulo chokumbira, kapena ngati iye ali wachikasu ngati dzungu, kapena ngati



iyе ali wabuluu ngati indigo, iye akhoza kupulumutsa moyo wanu pa kukupatsani inu magazi mmisempha. Koma inu musati muyike konse magazi a chinyama mwa inu.” Ndithudi, iyeyo ndi munthu.

<sup>143</sup> Kungoti chifukwa khungu limodzi linali lakuda, ndipo limodzi linalo labulauni, ndi limodzi linalo lachikasu, ndipo limodzi linalo loyera, izo ziribe kanthu kochita ndi izo. Baibulo linati, “Mulungu mwa gazi limodzi anapanga anthu onse.” Ndipo ndiko kulondola chimodzimidzi. Malo amene ife timakhalamo, kusintha kwa mitundu, analibe kanthu koti achite nazo izo. Mulungu anapanga a mmodzi—munthu mmodzi mafuko onse, magazi amodzi, mafuko onse chimodzimidzi.

<sup>144</sup> Mchaina; munthu wakuda sangakhoze kunena tsopano, munthu wakuda sangakhoze kunena tsopano, kuti, “Mchaina, iye—iye ndi wachikasu, ine ndiribe chochita naye iye.” Iye ndi m’bale wanu. [M’bale Branham agogoda pa guwa kangapo—Mkonzi.] Ndipo iwe munthu woyera siungakhoze kunena kwa munthu wachikasu kapena munthu wakuda, wina aliyenseyo, “Ine ndiribe chochita ndi iwe” Iye ndi m’bale wako. Kulondola chimodzimidzi.

<sup>145</sup> Zindikirani tsopano, pano pali chimene chinachitika. Ine ndikukhulupirira, ndipo ine ndikhoza kuzithandizira izo mwa Baibulo, kuti ndi serpenti amene anachita izo. Serpenti ndiye munthu woswayo pakati pa chimpanzi ndi munthu. Chifukwa, mvetserani, zindikirani izi tsopano, kuti serpenti sanali wokwawa. Iye anali kwambiri “wochenjera” mwa zinyama zonse za kuthengo.

<sup>146</sup> Tsopano, ine ndinapita ndipo ndinakatenga madikishonare, lero, ochokera kulikonse, kuti ndikayang’anemo mawu awa, chimene mawu akuti *wochenjera* amatanthauza. Iwo amatanthauza “kukhala wochenjera, kukhala wothyathyalika,” ndipo, kutanthauzira kwabwino kwa—kwa Chihebri (kuchokera ku m-a-h-a-h, mahah) kumatanthauza “kukhala nacho chidziwitso choona cha zofunika za moyo.”

<sup>147</sup> Tsopano tiyeni tipenye izi miniti yokha. Iye ndi wochenjera, wothyathyalika, komabe iye akutchedwa “serpenti.” Koma, kumbukirani, iye anali chinthu chochenjeretsetsa chimene chinalipo, ndipo chofanana kwambiri ndi munthu kuposa china chirichonse chimene chinalipo mmunda; chapafupi kwa munthu wokhalapo. Iye sanali chokwawa ayi. Themberero linamupanga iye chokwawa. Ndipo iye anali...Baibulo linati iye anali wokongola kwambiri wa zonse.

<sup>148</sup> Ndipo ngakhale themberero silinatenge kukongola kwake konse kukuchotsa; komabe mangamanga aulemerero a njoka ndi okongola, ndipo chisomo chake ndi kuthyathyalika kwake. Ngakhale themberero silinasunthe izo nkuzichotsa. Koma, kumbukirani, Mulungu anamuwuza iye kuti miyendo yake

ikanachoka ndipo kuti iye akanati azidzayenda ndi pa mimba yake. Ndipo inu simungakhoze kupeza fupa limodzi mwa njoka limene limawoneka ngati munthu, ndipo ndicho chifukwa sayansi yatayika. Koma ndi uyo apo.

<sup>149</sup> Mulungu anazibisa izo ku maso a anzeru ndi aluntha, ndipo analonjeza kuti adzawulule izo kwa ana aamuna a Mulungu, mu masiku otsiriza pamene ana aamuna a Mulungu ati adzawonetseredwe, pamene, “Ana aamuna a Mulungu amene ankasangalala ngakhale maziko a dziko asanayikidwe.” Pamene vumbulutso lalikulu la Umulungu ndi zinthu ziti zidzabweretsedwe pansi mu masiku otsiriza, Iye akanati adzawonetsere zinthu izi kupyolera mwa ana aamuna a Mulungu. Inu mukudziwa kuti Lemba limaphunzitsa zimenezo. Ndipo ndife pano. Ndicho chifukwa Mulungu akutsegulira zinthu izi kwa ife. Mulungu akuwabweretsa mwa ana Ake aamuna mu kuwonetseredwa. Iye akupita kudutsa malire a nzeru iliyonse ya umunthu, kutali mpaka mu mavumbulutso auzimu, ndi kulibweretsa Ilo pansi. Kodi ife sitinakhale tikuphunzitsa, mu Baibulo ili, “Pano ziri kwa iye amene ali nayo nzeru”? Osati zimene iye anaphunzira mu seminare ina; koma zimene iye anaphunzira pa maondo ake pamaso pa Mulungu, ndi chimene chinamukondweretsa Mulungu kuti amupatse iye. Ana aamuna a Mulungu, kukhala akuwonetseredwa!

<sup>150</sup> Pano pali serpenti, tsopano pano pali chimene serpenti anali; ine ndikupatsani inu kufotokoza kwanga kwa iye.

<sup>151</sup> Ife tiri ndi... ife tabwera pansi, kuchokera kwa chule, kupitirira mpaka kwa mbululu ija, ndipo kupitirira pansi ndi kupitirira, ndi *zakuti-ndi-zakuti*, mpaka inu potsiriza munafika kwa nyani, kwa chimpanzi. Ndipo kuchokera kwa chimpanzi, tsopano ife talumpha kuchoka kwa chimpanzi kufika kwa munthu, ndipo ife tikudabwa chifukwa chiyani.

<sup>152</sup> “Chabwino,” sayansi imanena kuti, “tsopano dikirani! Ife tikhoza kubalitsa mkazi kwa nyani ndi kwa chimpanzi, ndiyeno mosinthanitsa, mwamuna kubalitsa kwa chimpanzi.” Izo sizingagwire ntchito. Kubalitsa iye kwa chinyama china chirichonse; izo sizingagwire ntchito. Magazi sangasakanizikane; kutenga magazi anu, ali onse palimodzi magazi osiyana, palimodzi.

<sup>153</sup> Pali magazi ena pakati apa, ndipo iwo sangakhoze kuchipeza chinyamacho. O, aleluya, ine ndikuyamba kumverera mwachipembedzo pakali pano. Zindikirani. Chifukwa chiyani? Mulungu anazibisa izo kwa iwo. Palibe fupa mwa njoka limene limawoneka ngati fupa la umunthu. Iye anachiyika chinthucho kutali kwambiri mwakuti icho sichikanakhoza kupezedwa ndi munthu wanzeru.

154 Ndipo ine ndikuwonetsani inu kumene munthu wanzeru ameneyo amachokera, kumene—kumene iye aliko, mulimonse. Mwaona, iye sangakhoze kubwera kupyolera mu zimenezo.

155 Izo ziyenera kubwera mwa vumbulutso, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa . . .” “Pa thanthwe ili ine ndidzamangapo Mpingo Wanga; ndipo zipata za ku gehena sizingakhoze kulakika motsutsa iwo,” vumbulutso lauzimu. Motani—anadziwa motani Abele kuti apereke mwanawankhosa, mmalo mwa Kaini wopereka zipatso za kumunda? Izo zinawululidwa mwauzimu kwa iye. Iwe sumazipeza izo mwa maseminare. Iwe sumazipeza izo kupyolera mu zipembedzo. Iwe umazipeza izo kuchokera Kumwamba.

156 Tsopano penyani serpenti, serpenti iyi imene inali poyamba. Tiyeni tijambule chithunzi cha iye tsopano. Iye ndi munthu wamkulu kwambiri. Iye ali pakati pa chimpanzi ndi munthu. Ndipo, serpenti; mdierekezi, Lucifara, ankadziwa kuti uko kunali magazi okha amene akanakhoza kusakanizikana ndi magazi a munthu awa, munthu yekhayo amene iye akanakhoza kuchita naye. Iye sakanakhoza kuchita ndi chimpanzi, magazi amenewo sakanakhoza kusakanizikana. Iye sakanakhoza kuchita ndi zinthu zosiyana. Iye sakanakhoza kuchita ndi nkhosa. Iye sakanakhoza kuchita ndi kavalo. Iye sakanakhoza kuchita ndi chinyama chirichonse; iye anayenera kuti achite ndi serpenti iyi.

157 Tiyeni timutenge iye tsopano ndi kuwona chimene iye amawoneka ngati. Iye ali munthu wamkulu kwambiri, chimphona cha mbiriyakale yoyambirira. Ndiko kumene iwo amapeza mafupa aakulu awa, ndipo ine ndikuwonetsani inu izi mu Baibulo. Tsopano penyani mwacheru. Chabwino. Munthu wamkulu kwambiri uyu, tiyeni tinene kuti iye—iye anali utali wa mapazi khumi, mapewa aakulu kwambiri; ankawoneka basi ngati munthu. Ndipo magazi ake; atatha kubwera pansu, kukweranitsa nyama imodzi kwa imzake. Inu mukhoza kusemphanitsa zinyama. Ndipo izo zinapitirira kumatenga magazi apamwamba, mawonekedwe apamwamba a moyo, mawonekedwe apamwamba, mpaka izo zikukwera mpaka ku dera la munthu. Koma kulumikiza kotsiriza apa, pakati apa, chinadulidwa kuchokapo. Ndi angati amene akudziwa kuti sayansi siyingakhoze kupeza chilumikizo chosowacho? Nonse a inu mukudziwa zimenezo. Chifukwa chiyani? Apa iye ali, serpenti. Apa iye analipo, munthu wamkulu kwambiri.

Ndipo mdierekezi akubwera pansu, tsopano, iye akuti, “Ine ndikhoza kudzoza.”

158 Tsopano pamene inu mupita mukuyang’ana pa akazi, ndi kumachita nawo akazi, kumbukirani, inu muli odzozedwa ndi mdierekezi; uyo si mkazi wanu yemwe.

<sup>159</sup> Zindikirani, tsopano, mdierekezi anabwera pansi ndipo analowa mwa serpenti. Ndipo iye anamupeza Eva mu munda wa Edeni, wamaliseche, ndipo iye anayankhula za chipatso pakati. *Pakati* amatanthauza “chirikati,” ndi zina zotero; inu mukumvetsa, mu gulu losakanizikana. Ndipo iye anati, “Tsopano, ndi chokongola. Ndi chabwino kwa diso.” Ndipo kodi iye anachita chiyani? Iye anayamba kupanga chikondi kwa Eva, ndipo iye anakhala naye iye, ngati mwamuna wake.

<sup>160</sup> Ndipo iye anawona kuti icho chinali chokondweretsa, kotero iye anapita ndipo anakamuuza mwamuna wake, koma iye anali kale ndi pakati pa Satana.

<sup>161</sup> Ndipo iye anabala mwana wake woyamba wamwamuna, amene dzina lake linali Kaini, mwana wa Satana.

“Tsopano,” inu mukuti, “ndiko kulakwitsa.”

<sup>162</sup> Chabwino, ife tingopeza ngati ziri zolakwika kapena ayi. “Ndipo Ine ndidzayika udani pakati pa mbewu yako ndi mbewu ya serpenti.” Chiyani? Mbewu ya serpenti! Iye anali nayo Mbewu, ndipo iye anali nayo mbewu. “Ndipo Iye adzavulaza mutu wako, ndipo iwe udzavulaza chidendene Chake.” Ndipo *kuvulaza*, pamenepo, kukutanthauza, “kupanga Chitetezero.” Tsopano ndi imeneyotu “mbewu” yanu ya serpenti.

Tsopano, zindikirani, apa pakutulukira amuna awiri awa.

<sup>163</sup> Tsopano, serpenti uyu, pamene iye anayima apo, chimphona chachikulu kwambiri ichi cha munthu chinayimirira pamenepo, iye anali wolakwa pa kuchita chigololo ndi mkazi wa Adamu. Kodi tchimo liri kuti lero? Ndi chiyani chimene chikupangitsa zinthu momwe izo ziliri lero? Tsopano, ine—ine. . . Ndithudi inu mukhoza kugwira chimene ine ndikukamba za icho. Ndipo apo icho chinali.

Ndipo pamene iye anatero, Mulungu anati, anayamba kumuyitana Eva ndi Adamu.

Ndipo iye anati, “Ine ndinali maliseche.”

Ndipo Iye anati, “Ndani anakuwuzza iwe kuti iwe unali maliseche?”

<sup>164</sup> Ndiye iwo anayamba, kachitidwe ka ankhondo, kupatsirana chidebe. Anati, “Chabwino, mkazi yemwe Inu mwandipatsa ine, wachita icho. Iye anali mmodzi amene anandikakamiza ine.”

<sup>165</sup> Ndipo iye anati, “Serpenti anandipatsa ine apulo?” Chabwino, mlaliki, fika pafupi kwa iwemwini.

<sup>166</sup> Iye anati, “Serpenti anandinyenga ine.” Kodi inu mukudziwa chimene *kunyenga* amatanthauza? Icho chimatanthauza “kuyipitsidwa.” Ndipo iye anali. Mdierekezi sanamupatse iye apulo konse. “Serpenti wandinyenga ine.”

Ndiyeno themberero linabwera.

167 Iye anati, “Chifukwa iwe unamvetsera kwa serpenti mmalo mwa mwamuna wako, iwe wawuchotsa Moyo kuchoka mu dziko. Ndipo iwe udza—iwe udzachelukitsa zowawa zako; ndipo kukhala ndi pakati kwako kudzakhala kwa mwamuna wako,” ndi zina zotero.

168 “Ndipo chifukwa iwe unamvetsera kwa mkazi wako, mmalo mwa Ine (Ine ndinakutenga iwe kuchokera ku fumbi; mtundu wapamwamba), kubwerera ku fumbi iwe upita.”

169 “Ndipo, serpenti, chifukwa iwe wachita zimenezo, miyendo yako ikuchoka. Pa mimba yako iwe uziyenda, masiku onse a moyo wako. Ndipo iwe udzakhala ukudedwa. Ndipo fumbi lidzakhala chakudya chako.” Ndi zimenezotu. Apo pali chilumikizo chosowacho.

170 Tsopano apa pakubwera Kaini. Tiyeni tiwone zibadwazo. Apa pakubwera Kaini. Kodi iye ali chiyani? Iye ndi munthu wamalonda wothe yathyalika. Iye amalima minda. Wanzeru, waluntha; wachipembedzo, wachipembedzo kwambiri; penyani zake—penyani zotsatira zake tsopano. Mungosuntha ndi ine kwa utali wa maminiti yokha pang’ono motalikirapo.

171 Apa iye akubwerapo. Iye akudziwa iye ndi wakhalidwe. Iye akufuna kupita ku tchalitchi. Iye akumumangira iye tchalitchi, akumupangira iye chopereka. Akubweretsa guwa, ndi zonse. Kumanga guwa, kuyika maluwa ake pa ilo. Kuyikapo munda, zipatso za kumunda, kuzipereka izo kwa Mulungu. Anati, “Landirani izo Inu, Ambuye. Ine ndikudziwa kuti ife tinadya maapulo, ndicho chimene chinapangitsa izo.” Ena a osokonezeka ake ali nalo lingaliro la mtundu womwewo. Akusonyeza kumene iwo anachokerako. Anabweretsamo maapulo ake, kuchokera ku munda, kuziyika izo pamenepo, anati, “Izi zipanga chitetezero.”

Mulungu anati, “Iwo sanali maapulo.”

172 Koma, mwa vumbulutso lauzimu, Abele anadziwa kuti iwo anali magazi. Kotero iye anabweretsa mwanawankhosa, anadula khosi lake, ndipo iye anafa.

173 Ndipo Mulungu anati, “Ndiko kulondola. Ndicho chimene chinachita izo. Iwo anali magazi.” Inu mukudziwa magazi amene ine ndikuwakamba. Chabwino. “Iwo anali magazi amene anachita izo.”

174 Tsopano penyani. Ndiyeno pamene Kaini anamuwona m’bale wake woyera-wodzigudubuza kuti anali atalandiridwa pamaso pa Mulungu, ndipo zizindikiro ndi zodabwitsa zinali zikuchitika kumusi uko, iye anakhala wansanje naye iye. Iye anati, “Ife tiyimitsa zinthu izi pakali pano.” Penyani pa abale ake, penyani pa ana ake, alipo lero. “Tsopano, ine ndine wanzeru kuposa iye ali,” kotero iye anakhala wokwiya. Kodi *kukwiya*ko kunachokera kuti? Kodi inu mukanakhoza kunena kuti kukwiya . . . Iye anamupha m’bale wake. Iye anali wakupha.

<sup>175</sup> Kodi inu mukanakhoza kumutcha Mulungu wakupha? Ndipo Adamu anali mwana wamwamuna wa Mulungu. Baibulo linanena, kuti, “Adamu anali mwana wamwamuna wa Mulungu,” kuyamba kwangwiwo kumbuyo uko. Adamu anali mwana wamwamuna wa Mulungu. Ndipo nsanje imeneyo ndi kuyipidwa, ndi chirichonse, sizikanakhoza kubwera kuchokera mu mtsempha wangwiwo uwo.

<sup>176</sup> Izo zinayenera kubwera kupyolera mu malo ena. Ndipo izo zinabwera kupyolera mwa Satana, yemwe anali wakupha, kuyamba ndi kuyamba. Baibulo linati, “Iye anali wabodza ndi wakupha, kuyamba ndi kuyamba.” Ndipo apo izo ziri. Ndipo iye anamupha m’bale wake.

<sup>177</sup> Ndipo icho chinali choyimira cha imfa ya Khristu. Ndiye, kuchokera kumeneko, zooni, Iye anawukitsa Seti kuti atenge malo ake. Imfa, kuyikidwa mmanda, ndi kuwuka kwa Khristu.

<sup>178</sup> Ndipo penyani, ndiye, apa pakubwera zimphona zanu. Ndiye Kaini anapita ku dziko la Nodi. Ngati adadi ake anali chimphona chachikulu kwambiri cha munthu, nanga Kaini akanakhala monga chiyani? Adadi ake. Ndipo iye anapita ku dziko la Nodi, ndipo anatenga mmodzi wa alongo ake.

<sup>179</sup> Njira yokha imene iye akanakhoza kuchitira. Uko kulibe akazi enanso amene akanakhoza kubwera, koma kokha kupyolera mwa Eva. Iwo amanena kuti iwo anali ndi ana aamuna makumi asanu ndi awiri ndi ana aakazi. Ngati—ngati uko kunalibe wamkazi. . . Baibulo silimalemba akazi pamene iwo anali kubadwa, amuna okha. Ndipo pamene, ngati uko kunalibe akazi enanso kuposa Eva, pamene iye anafa, mtundu wa anthu ukanasiya kukhalapo. Iye amayenera kukhala ndi ana aakazi. Ndipo iye amayenera kuti akwatire mlongo wake yemwe.

<sup>180</sup> Iye anapita ku dziko la Nodi ndipo anakatenga—ndipo anatenga mkazi wake. Ndipo pamene iye anamukwatira iye kumeneko, uko ndi kumene iwo anayambitsa zimphona zazikulu zija, zimene zinali ana aamuna akugwa a Mulungu; amene anadza kupyolera mwa abambo wawo, mdierekezi, kupyolera mwa Kaini. Apo pali chilumikizo chanu chosowa.

<sup>181</sup> Ndipo ipenyeni mbewu ya serpenti. Tsopano penyani. Kumbukirani, mbewu ya serpenti ndi yachipembedzo. Ipenyeni iyo ikuyamba kusuntha tsopano, kwa maminiti pang’ono. Pano iyo ikupita, mbewu ya serpenti. Ndi chiyani chinachitika kwa iwo? Tsopano ndiroleni ine ndingowerenga chinachake pano, ine ndachilemba kumene madzulo ano.

<sup>182</sup> Ndi chiyani chimene chinabwera kupyolera mu mzere wa Abele? Mvetserani kwa izi. Chabwino. Motsatira panadza Abele. Atachoka Abele kubwera Seti. Atachoka Seti kubwera Nowa. Atachoka Nowa kubwera Shemu. Atachoka Shemu kubwera Abrahamu. Atachoka Abrahamu kubwera Isaki. Atachoka Isaki

kubwera Yakobo. Atachoka Yakobo kubwera Yuda. Atachoka Yuda kubwera Davide. Atachoka Davide kubwera Khristu, ku ungwiro.

<sup>183</sup> Penyani kumbuyo uko momwe Mzimu wa Mulungu unakhalira mwa Abele. Yang'anani momwe Iwo unakhalira mwa Seti. Yang'anani momwe Iwo unakhalira mwa Yuda. Yang'anani momwe Iwo unakhalira mwa Davide. Yang'anani pa Mzimu womwewo ukuyitanira kunja, kupyolera mu mbewu yachilungamo iyo, njira yonse mmusimo. Ziribe kanthu chimene iwo anachita, iwo anali okonzedweratu.

<sup>184</sup> Yang'anani pa Yakobo, wauve...Ine sindikunena izi kupyolera mu kusinjirira. Koma Yakobo, shasha wamng'ono, akukangamira pansu pa chipsyepsye cha chikhoto cha amayi ake nthawi zonse; kumathamanga pozungulira, mnyamata wamng'ono wachikazi. Kuyika zinthu pa iye, anapita ndi kukawanyenga abambo ake, kuti akapeze dalitso; koma ilo linaperekedwa kwa iye asanayikidwe maziko a dziko. Zedi, iwo anatero.

<sup>185</sup> Anapita kunja uko ndipo anakanama kwa apongozi-ake aamuna; ndipo anatenga timitengo tina tamaangamaanga, timitengo ta popula, ndi kutiyika ito mmadzi, kuti aziwopsyeze ng'ombe izi pamene izo zinali ndi bere; kuti azipangitse izo kuti zibale ng'ombe za maangamaanga, koteru kuti iye akhoze kunyenga ndi kuzitenga ng'ombe zimenezo. Mulungu anamudalitsa iye mu zimenezo. Ndiko kulondola.

<sup>186</sup> Tsoka kwa aliyense amene ati anene chirichonse motsutsa Yakobo. Inu mukudziwa chiyani—inu mukudziwa chimene mneneri wabodza ananena...Kapena, iye anali akulosea mlondola. Balaamu, iye anati, “Yense yemwe amudalitsa iye adzadalitsidwa, ndi yense amene amutemberera iye adzatembereredwa.”

<sup>187</sup> “Ine ndinakutenga iwe, Yakobo. Ine ndinamupeza iye ngati ...ngati mu dziko lachirendo. Ndipo monga mphungu ikasula chisa chake, Ine ndinamukasula iye ndipo ndinamutulutsa iye kunja.” Aleluya! [M'bale Branham awombetsa manja ake limodzi katatu—Mkonzi.] “Osati mwa mphamvu, osati mwa nyonga, koma mwa Mzimu Wanga, atero Ambuye.”

<sup>188</sup> Penyani izo zikubwera pansu ku ungwiro uwo. Mzimu umenewo unagwira ntchito mpaka ku ungwiro mwa Khristu, mpaka kupyolera mwa wina aliyense wa M'badwa, kumabwera mpaka pansu. Ziribe kanthu chimene iwo anachita, chimene iwo ananena, chimene iwo anachita, iwo anali mwamtheradi mbewu ya wolungama.

<sup>189</sup> Ndipo, apa, pamene Abrahamu wolungama... Ulemerero! O, ine ndikungomverera bwino kwenikweni. Pamene Abrahamu

wolungama anakomana ndi Melkizedeki, Yemwe anali Mulungu Iyemwini!

<sup>190</sup> Melkizedeki anali ndani? “Mfumu ya Salemu, yemwe ali Mfumu ya Yerusalemu, Mfumu ya mtendere. Iye analibe atate. Iye analibe amayi. Iye analibe konse chiyambi cha masiku, ngakhale mapeto a moyo.” Yense Yemwe Iye ali, Iye akadali moyo. “Iye sanabalidwe konse. Iye sadzafa konse. Iye analibe konse atate kapena amayi. Iye analibe konse chiyambi cha masiku, kapena mathero a moyo.” Ndiwuzeni ine Yemwe iye anali. Mulungu Wamuyaya; mu chimene ife timachitcha . . .

<sup>191</sup> O, ine ndayiwala kokha chimene inu mumachitcha icho pakali pano. Fiofane, ndi chimene icho chiri. Basi mofanana. . . Osati nthano; komabe ndi chinachake basi chimene chawonetseredwa. Monga Iye anabwera kwa Abahamu mu hema kumtunda kuja, monga mngelo, ndipo analosera, ndipo anamuza Sarah kuti iye anaseka, kuseri kwa Iye, ndi zina zotero. Chinthucho, chinthu chomwecho.

<sup>192</sup> Ndipo Iye anali apa. Iye anakomana ndi Melkizedeki. Ndipo agogo- . . . agogo-aamuna a bambo ake Abrahamu, mu mbewu ya wolungama, anapereka zachikhumi kwa Melkizedeki; ndipo izo zinayikidwa kwa muzukulu wa mwana wake pansu apa, mbewu ya wolungama.

<sup>193</sup> Tsopano apa pakubwera mbewu ya—ya serpenti. Tsopano, kumbukirani, padzakhala pali udani, nk'hondo pakati pawo.

<sup>194</sup> Mbewu ya serpenti ikubwera motsatira, ndipo kodi iyo ikubala chiyani? Tsopano tiyeni titenge zaka zoyamba pang'ono. Tsopano penyani chimene chikuchitika uko. Ife tiwerenga izo uko, chifukwa ine ndangofufuza kumene izo. Mbewu ya serpenti inabala Kaini. Kaini anapita ku dziko la Nodi, anakabala zimphona, ndiyeno iwo anabwera ku dziko la Nowa.

<sup>195</sup> Iwo anali anzeru, ophunzira, anthu aluntha. Ndi kulondola uko? Iwo anali omanga, oyambitsa, asayansi; osati kupyolera mu mbewu ya wolungama, koma kupyolera mu mbewu ya Satana, serpenti. Iwo anali anthu otero monga—monga asayansi, ndi omanga, ndi anthu aakulu, ophunzitsa. Lemba limanena choncho. Iwo ankagwiritsa ntchito mkuwa. Iwo ankagwiritsa ntchito chitsulo. Iwo ankagwiritsa ntchito ziwaya. Iwo ankapanga zinthu. Iwo ankawumba ziwaya zosiyana, ndi kumanga nyumba, ndi zina zotero. Lemba limanena choncho. Ndipo iwo anali onyoza pa Mbewu ya mkazi, Nowa, wolungama. Ndi kulondola uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>196</sup> Tiyeni tiwatsatire iwo mopitirira pang'ono. Ndiye, ife tiwafikitsa iwo ku chombo, chirichonse chinawonongedwa. Anafika mu chisakanizikiro chotero cha tchimo, ndipo iwo anatenga kulamulira, ndipo anzeru kwambiri ndi aluntha. Mpaka, Mulungu anayang'ana pansu, panalibe apo ochuluka kwambiri amene anatsalira, kotero Iye anangomutengera Nowa



ndi banja lake mu chombo, ndipo anavumbitsira madzi pansi ndipo anawononga chinthu chonsecho. Anamutengera Enoki mmwamba, nthawi isanafike. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Uko kunali mbewu zonse, pafupifupi mbewu zonse; koma iye ali nacho cholinga chomwe chinayenera kuti chikwaniritsidwe.

<sup>197</sup> Tsopano, Nowa ndi ana ake aamuna, amene anatulukira, Hamu, Shemu, ndi Yafeti, anatulukira mu mzere wa wolungama.

<sup>198</sup> Kodi mbewuyo inawolokerako motani? Mbewuyo inabwera mpaka mu chombo, monga momwe iyo inachitira pachiyambi, kupyolera mwa mkazi, akazi awo. Iwo anyanyamula mbewu ya Satana, kudzera mu chombo; basi monga Eva anyanyamula mbewu ya Satana, kuti akabale Kaini, kupyolera mwa mkazi.

<sup>199</sup> Inu mumawayika akazi awo mu nsanja zanu kukhala alaliki, Baibulo limatsutsa izo! Paulo anati, “Ngati munthu aliyense adziyesa yekha kuti ali mneneri, kapena ngakhale wauzimu, msiyeni iye avomereze kuti chimene ine ndikulemba ndi malamulo a Ambuye; koma ngati iye ati akhale wosadziwa, ingomusiyani iye kuti akhale wosadziwa.”

<sup>200</sup> Ndicho chifukwa chimene ine ndinatulukira mu mpingo wa Baptisti kumusi kuno. M'bale Fleeman anali pano kanthawi kapitako; ine ndikuganiza iye anali kumeneko usiku umenewo. Dr. Davis anati, “Iwe uyima apa ndi kuwadozoza akazi awa akhale alaliki.”

Ine ndinati, “Ine sindidzachita ayi zimenezo. Ayi, indedi.”

Iye anati, “Chabwino, ine ndikuponyera iwe kunjia.”

<sup>201</sup> Ine ndinati, “Ine ndaponyeredwera kunjia ndi chabwino.” Ine ndinati, “Awa ndi Mawu a Mulungu, ndipo Iwo amatsutsa chinthucho. Ndipo ine sindingakhoze kunyamulira mmwamba chimene Mulungu achitsutsa.” Ayi, bwana.

<sup>202</sup> Onse omwe achita izo, akusonyeza kuti iwo ali aphunzitsi abodza, aneneri abodza. Baibulo linati iwo akanadzakhala. “Kunyenga osankhidwa omwe ngati nkotheka.” Ndi inu apo.

<sup>203</sup> Zindikirani izi tsopano. Ndipo kuchokera pamenepo, ndiye, pakubwera Hamu, Hamu ndi mkazi wake, ndi iwo. Iye anali nalo themberero litayikidwa pa iye. Kuchokera kwa Hamu kukubwera Nimrodi, amene anamanga Babeloni. Kuchokera ku Babeloni kunadza mpingo wa Katolika, chiyambi cha iwo. Zinabwera mpaka mmusi kupyolera mwa Ahabu. Zinabwera mpaka mmusi kuchokera kwa Ahabu, mpaka kwa Yudasi Iskarioti; anamarizitsa izo, wotsutsa-Khristu.

<sup>204</sup> Ndipo mu masiku otsiriza awa, pano pali mzimu wa wotsutsa-Khristu ndi Mzimu wa Khristu. Mzimu wa otsutsa-Khristu, ukunena kuti, “Masiku a zozizwitsa anapita.” Mzimu wa Khristu, ukuti, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Mzimu wa wotsutsa-Khristu ukuti, “Izo

sizipanga kusiyana kulikonse ngati iwe wabatizidwa mwa 'Atate, Mwana, Mzimu Woyera,' kutsanuliridwa, kukonkhedwa, chirichonse chimene chiri, izo zikutanthauza chinthu chomwecho." Baibulo linanena kuti Mulungu ndi wosalephera, ndipo Iye sangakhoze kusintha. Nndani yemwe inu muti mumutumikire? Izo ziri kwa inu.

<sup>205</sup> Tsopano inu mukuti, "Kodi iwo angakhoze kumakhala limodzi? Inu munati, kuti, muja mu chombo chija, M'bale Branham, inu munali nawo mmenemo onse Hamu ndi Seti." Ndiko kulondola, kulondola chimodzimodzi. Hamu anali woyipa. Seti anali wachipembedzo ndi wolungama. Chabwino.

<sup>206</sup> Tiyeni timutsatire Hamu. Chabwino, tsopano, muli Hamu ndi Seti mu chombo chomwecho; mmodzi wolungama, ndi winayo wosalungama. Munali khwangwala ndi nkunda mu chombo chomwecho. Kunali Yudasu ndi Yesu mu mpingo womwewo. Kunali wotsutsa-Khristu ndi Mzimu Woyera mu mpingo womwewo.

<sup>207</sup> Ndipo, lero, mizimu yomweyo ikugwira ntchito. "Kukhala nawo mawonekedwe aumulungu, achipembedzo kwambiri, koma okhala nawo mawonekedwe aumulungu ndi kumakana Mphamvu yakeyo; kwa oterowo tembenukirani kumbali." Mzimu Woyera, ukunena kuti, "Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse." Ndi mbali iti yomwe inu muti musankhe?

<sup>208</sup> Wotsutsa-Khristu akunena kuti *Ili* ndi bukhu chabe la chikhulupiriro. [M'bale Branham akusonya Baibulo lake—Mkonzi.] "Ife tizibwereza Chikhulupiriro cha Atumwi." Ine ndikutsutsa mlaliki aliyense kuti andiwuze ine pamene Chikhulupiriro cha Atumwi chikupezeke mu Baibulo: "Ine ndimakhulupirira mwa Mulungu, Atate Wamphamvuzonse, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi; ndi Yesu Khristu, Mwana Wake. Ine ndimakhulupirira mu Mpingo Woyera wa Roma Katolika, chiyanjano cha oyera." Inu mumazipeza kuti zimenezo mu Baibulo? Ndipo komabe inu mukumabwereza izo mu mpingo yanu yayikulu ya Methodistu ndi Baptisti. Ndi chiphunzitsa cha mdierekezi, ndipo aneneri abodza akuphunzitsa zimenezo.

<sup>209</sup> Ndipo ine ndikuyembekeza kuti ine sindikupweteka kumverera kwanu, koma ine ndikukhomerera izo kwa kachisi uyu. Inu pano pa Branham Tabernacle, talikirani kwa zinthu zoterozo. Chirichonse chimene chimakhulupirira mu chiyanjano cha oyera ndi zamizimu. "Pali mkhalapakati mmodzi yekha pakati pa Mulungu ndi munthu, ndipo ameneyo ndi Mwamuna Yesu Khristu." [M'bale Branham agogoda pa guwa kanai—Mkonzi.] Sindikusamala ndi Amaria angati amene alipo!

<sup>210</sup> Mwaona momwe mbewu ya mkazi imeneyo kumbuyo kumeneko inachitira? Mwaona momwe mbewu ya mkazi inanyamulidwira mmenemo?

<sup>211</sup> Penyani pa lero, mu Amereka. Amereka ndi mbewu ya mderekezi. Ndi chiyani icho? Iye ndi fuko la mkazi. Inu mwamvapo kuti, “Ili ndi dziko la mkazi.” Ndiko kulondola. Ndi fuko la mkazi. Iwo amayambitsa kachitidwe.

<sup>212</sup> Ine ndinapita cha kuno, osati kale litali, mu Switzerland. Akazi akuti . . . Mkazi mmodzi wamng’ono, wa Mzimu Woyera anati, “Inu mukudziwa, ngati ine ndipita mu Amereka, iwo amati akazi ali nawo ufulu.”

<sup>213</sup> Ine ndinati, “Ndiroleni ine ndikuwuzeni inu chimene izo zikulunjika.” Ndipo ine ndinayamba kumuuzza iye.

Iye anati, “O, chifundo, ine sindikufuna chirichonse cha izo.”

Ine ndinati, “Ndiko kumene icho chikulunjika.”

Inu mukudziwa, kuti iwo samachita zinthu uko monga iwo amachitira kuno.

<sup>214</sup> Ndi chiyani icho? Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu kuti Amereka ndi mkazi. Pa ndalama yathu pali chithunzi cha mkazi. Chirichonse muno ndi mkazi.

<sup>215</sup> Ndiwuzeni ine, mulibe malo ogulitsirako mowa okwanira mu dzikoli, bwezi ata . . . Inu mukhoza kuyika malo ogulitsirako mowa makumi anai mu mzinda uno, ndi kuyika achiwerewere atatu, akazi owoneka-bwino amene akudzipotola okha uko pa msewu; iwo atumiza miyoyo yambiri ku gehena, powakhumbira iwo, kuposa malo ogulitsirako mowa amene inu mukanakhoza kuwayika mu mzinda. Ndiko kulondola chimodzimidzi.

<sup>216</sup> Ndi ndani uyo ndiye? Ndi mkazi. Iye ndi chiyani? Iye ndi mulungu wa Amereka.

<sup>217</sup> Atengeni ena a asewero pa kanema aakulu awa, ndi kufika kuno, kukwatiwa kanai kapena kasanu, kumakhala ndi amuna atatu kapena anai osiyana pa nthawi yomweyo; ndipo ena a magazini awa akuwayalutsa ndi kuwawuza iwo, kujambula zithunzi zawo ali maliseche kunjika kuno. Ndipo inu asungwana aang’ono nkuchiyika icho ngati chitsanzo chanu, (chifukwa chiyani?) chifukwa mayi anu musanabadwe inu, mwinamwake, agogo anu aakazi musanabadwe inu. Inu mukuwona kumene mbewu ya serpenti iyo ikugwirako ntchito? Ndithudi, izo ziri.

<sup>218</sup> Ndipo kodi iyo yachita chiyani? Ngati kusayeruzika ndi kuchezeredwa kwa mibadwo khumi ndi inai, pansu pa lamulo, kusayeruzika kudzakhalala chiyani ngati kutachezeredwa mu tsiku lino, pamene mbewu ya wosalungama yatsala pang’ono kutsirizidwa? Ndipo Mulungu anati idzabwera nthawi iyo, ngati Iye akanapanda kudula ntchito mofupika, pakanakhala palibe aliyense wa iyo yosiyidwa. Iye tiri pa nthawi yotsiriza. Sakani chirungamo usikuuno; pitani kupyola mu mzinda!

<sup>219</sup> O, iwe umawapeza mamembala a mpingo omvera basi kwa Abaptisti ndi Apresbateria, ndi ena otero, monga momwe izo zingakhoze kukhalira. Koma iwo alibe chochita chinanso ndi

Mulungu kuposa momwe kalulu angavalire nsapato za chisanu. Sadziwa kanthu za Izo! Chonse chimene iwo amadziwa... Kodi ndinu Mkhristu? “Ine ndine Mkatolika.” Kodi ndinu Mkhristu? “Ine ndine wa Baptisti.” Kodi ndinu Mkhristu? “Ine ndine wa Presbateria.” Kodi ndinu Mkhristu? “Ine ndine wa Chipentekoste.” Icho chiribe kanthu kochita nacho Icho.

<sup>220</sup> Ndiwe Mkhristu chifukwa Mulungu, mwa chisomo Chake, anakupulumutsa iwe. Ndipo iwe ukudziwa za Izo. Ndipo chinachake chasintha moyo wako, mwakuti iwe ukukhala mosiyana. Ndipo ndiwe munthu watsopano ndi chirengedwe mwa Khristu Yesu. Ndithudi.

<sup>221</sup> Koma inu mukuona kumene kuli mbewu ya serpenti? Inali chiyani mbewu ya serpenti? Chigololo. Kodi inu mukutsatira? Chigololo ndi Eva. Nchiyani chinachitika kwa icho? Nchiyani chimene chinabweretsa izo? Ndi chiyani icho usikuuno?

<sup>222</sup> Yang’anani mmbuyo kutsidya, zaka pang’ono zapitazo, pamene nyimbo yoyamba inatuluka. Inu anthu achikulirepo, pamene. . . Iwo anakonda kuzipima nyimbo iwo asanati azilole izo kuti ziyimbidwe pa wailesi. Ndipo imodzi yoyamba imene inatuluka, inali ija, “Funyululani izo, asungwana, funyululani izo, kuwonetsa mawondo anu okongola,” ndi zonse monga choncho. “Kuwaseka abambo ndi amayi, ndi kuwapatsa iwo onse ‘ho-ho-ho!’” Ndiyo imodzi yoyamba imene iwo anayilola kuti idutse chozemberamo. Ndi kuti kodi inu mukuganiza kuti mwamunayo ali usikuuno amene analemba nyimbo imeneyo? Iye anafa.

<sup>223</sup> Inu mukuganiza chiyani za Clara Bow, yemwe anatuluka koyamba ndipo anati, “mokhota mowopsya,” ndi kudolola podzivula kumene kunatumiza miyoyo zikwi ku gehena? Ndi kuti inu mukuganiza kuti iye ali usikuuno? Iye wakhala atafa kwa nthawi yayitali. Kodi ali kuti iye, ndi thupi lake lija? Wagona kutsidya, atawuma mu fumbi, ndipo tizirombo ndi mphutsi zadya kupyola mwa ilo. Ndipo moyo wake wagona kutsidya pamaso pa Mulungu wolungama.

<sup>224</sup> Ali kuti mwamuna yemwe anamutenga mkazi uja ndipo anamupangira zovala zowoneka-mwauve zakale zija zimene iwo amazivala, zowakankhira iwo onse kunjira mwa njira imodzi ndi imzake, ndi kusawakwanira iwo? Kotero iwo amachitiranji izo? Inu mumavaliranji zinthu za mtundu umenewo? Chifukwa inu mukufuna kuti mwamuna aziyang’ana pa inu, ndipo palibe njira yina yoti mutsimikizire izo. [M’bale Branham anagogoda pa guwa kangapo—Mkonzi.]

<sup>225</sup> Ndipo kodi inu mumadziwa kuti pamene inu muchita zimenezo, ndipo wochimwa wachikulire wina amayang’ana pa inu, inu mukudziwa chimene chachitika? Pa Malo Achiweruzo. . . Inu mukuti, “M’bale Branham, ine ndine basi woona kwa mwamuna wanga monga ine ndingakhoze

kukhalira.” Inu mudzawerengedwa wolakwa pa kuchita chigololo. Yesu anati, “Aliyense amene ayang’ana pa mkazi kuti amukhumbire iye wachita chigololo ndi iye kale mu mtima mwake.” Pamene mwamuna uyo ati akayankhire chifukwa chochita chigololo, ndi ndani yemwe ati akakhale amene anampangitsa icho? Momwe inu munadzivekera nokha ndi kudzipereka nokha.

<sup>226</sup> Tsopano, ine sindikutanthauza kunena kuti inu muyenera kumavala monga chinachake chimzake chochokera ku bokosi la amakezana. Koma, inu mukhoza kuwoneka mochuluka ngati dona.

<sup>227</sup> Ndipo kutuluka kunja kuno ndi kudzivula, akabudula anu aang’ono aafupi, ndi kumanga kaduwa pang’ono mozungulira iwo monga choncho; ndipo mwana wanu ali ndi maso ake ngati motayira ndudu, ndi ndudu mkamwa mwanu, mukuyenda uko mu msewu. Inu simumachita zimenezo kwa cholinga chabwino chirichonse. Inu mukhoza kukhala wosalakwa pa mfundooyo, koma mdierekezi akukugwiritsani inu ntchito kukhala chida basi monga iye anachitira ndi Eva.

<sup>228</sup> Ndi chifukwa chiyani liri fuko la mkazi? Chifukwa ilo likutsogolera kumene ku kulumulira kwa Chikatolika. Ndi chiyani icho lero? Inu simumawamva iwo akumutchula Yesu. “Tikuoneni Maria! Maria, mayi wa Mulungu! Cicilia Woyera!” Mitundu yonse ya oyera, oyera akufa. Kuno osati kale litali, uko mu. . .

<sup>229</sup> Ine ndinali uko ku Mexico, chaka chatha. Apa pakubwera mkazi wosawuka, akukhwekhweletsa. Mawondo ake, onse atakhwekhweletsedwa monga choncho, ndi khungu; akulira, ndipo atagwira manja ake. Ndipo abambo akuyenda motsatira, atanyamula ana aawiri ang’ono, iwo akulira; mayi akuzunzika chotero; chifukwa chakuti mkazi wina, yemwe iwo amamutcha woyera, anamwalira. Iwo anali nacho choyimikidwa chake pamenepo pa phiri. Bwenzi wake wina anamupha iye. Ndipo mwamsanga pamene iye aphedwa monga choncho, zoono, iye ndi woyera; iye anali Mkatolika. Kotero ndiye iye anali kupita, kuti akachite zakulapa; ndipo iye amayenera kukhwekhwelezeka mailosi awiri, pa miyala yoswedwa, kuti achite zakulapa.

<sup>230</sup> M’bale, ngati pali chinthu chimodzi chimene ine ndiyenera kuti ndichite, Yesu Khristu anafa mwachabe. Chisomo, ine ndapululumutsidwa; ndipo osati mwa—mwa inemwini, koma mwa chifuniro cha Mulungu, ndi mwa ubwino wa Mulungu.

<sup>231</sup> Atolankhani aja anandifunsa ine, anati, “Bambo Branham. . .” W—wamng’ono, mwana wakufa anali atabweretsedwa ku moyo, ndi zinthu pang’ono kumeneko. Akatolika zikwi makumi atatu. . .Ayi, ine ndikupempha kukhululukira kwanu. Iwo analipo zikwi makumi awiri. Zikwi makumi atatu kunali ku Afrika. Akatolika zikwi makumi awiri

analandira Khristu ngati Mpulumutsi wawo, pa nthawi imodzi, pamene izo zinachitika, nditayima mu Mzinda wa Mexico. Ndipo ansembe amenewo, iwo sakanakhoza kunena kanthu; ochuluka kwambiri, akanayambitsa chiwawa. Analipo ochuluka kwambiri pa mbaliyo. Kotero iye anati, “Bambo Branham, kodi inu mukukhulupirira kuti oyera athu akhoza kuchita chinthu chomwecho chimene inu mukuchita?”

<sup>232</sup> Podziwa chiphunzitsa chawo, ine ndinati, “Zedi, ngati iwo ali amoyo.” Mwaona? Kotero, iwe sungakhoze kukhala Mkatolika woyera mpaka iwe utafa, inu mukudziwa.

Kotero iye anati, “O, iwe sungakhoze kukhala woyera mpaka utafa.”

<sup>233</sup> Ine ndinati, “Mpati pamene inu mumawerenga zimenezo? Paulo anati, ‘Kwa oyera amene ali ku Efeso,’ ndi iwo amene ali oyitanidwa ndi Mulungu. ‘Kwa oyera amene ali ku Efeso,’ anali kuwerenga kalata yake; ndi oyera amene ali ku malo ena, ku Galatiya, ndi—ndi ‘oyera a ku Roma,’ ndi ena otero. *Oyera*, ‘iwo oyeretsedwawo.’ Nanga bwanji zimenezo?”

<sup>234</sup> Iye anati, “Ndithudi, tsopano, ife sityenera kuti tizitsutsana za Baibulo. Chifukwa, ife ndife mpingo, ndipo chimene mpingo unena. Ife sitimasamala chimene Baibulo likunena. Ndi chimene mpingo unanena.” Anati, “Ndiye lingaliro lanu ndi chiyani ndiye pa mpingo wa Katolika?”

<sup>235</sup> Ine ndinati, “Ine ndikanakhumba inu mukanati musandifunse ine zimenezo. Chifukwa inu mwandifunsa ine, tsopano ine ndikuuzani inu Choonadi.”

Anati, “Chabwino, ine ndikufuna inu mudiwuzze ine Choonadi.”

Ine ndinati, “Mawonekedwe apamwamba a zamizimu amene ine ndikuwadziwa.”

Iye anati, “Inu mumazipeza motani izo?”

<sup>236</sup> Ine ndinati, “Chirichonse chimene chimayankhulana ndi akufa ndi cha wamizimu.” Ine ndinati, “Ngati woyera ameneyo amayankhula moyankha, ndiye iye ali mu gehena. Chifukwa, iwo amene anawoloka njira, langa—Baibulo langa linanena kuti iye sakanakhoza kubwerera kumbuyo.” Ndiko kulondola. Ndipo ine ndinati, “Ngati iye ali, ngati iye anali woyera; ndi mdierokezi amene akuyankhula ngati woyera, ndipo iye sali woyerayo, pambuyo pa zonsezo.”

<sup>237</sup> Ndipo iye anati, “Chabwino, tsopano, miniti yokha.” Anati, “Inu mumayankhula ndi akufa, inunso.”

Ine ndinati, “Pati?”

Iye anati, “Yesu Khristu anafa.”

238 Ine ndinati, “Koma Iye anawuka kachiwiri. Iye sali wakufa. Koma Iye ali wamoyo, kuti azipangira zitetezero, ndipo mkhalapakati yekhayo pakati pa Mulungu ndi munthu.”

239 “Ine ndine Iye amene anali wakufa, ndipo ali wamoyo kachiwiri, ndipo ali wamoyo kwa nthawizonse mochuluka. Ine ndiri nawo mafungulo a imfa ndi hade.” “Aliyense amene afuna, mloleni iye adze ndi kumwa mwaulere kuchokera ku madzi a Moyo.” Mai! Uyo ndiye Mulungu wathu. Uyo ndiye Mulungu wathu.

240 Ndipo mbewu ya wolungama ili pafupi kuti ithe. Ukayankhula kwa anthu zokhudza zinthu izi. Ukayankhula kwa anthu zokhudza kubwerera mmbuyo ku njira ya Baibulo. Ukayankhula kwa anthu zokhudza zozizwitsa. Ukayankhula kwa anthu zokhudza izo. Wao “Mpingo sumakhulupirira Zimenezo,” kotero iwo ali ana a pathengo, kwa Mulungu. Baibulo linati ngati ife sitingakhoze kupirira mazunzo ndi mayesero, zonyodola, ndi kutchedwa oyera-odzigidubuzi” ndi zina zotero, monga choncho; ngati iwe sungakhoze kupirira izo, iwe ndi mwana wathengo, ndipo osati ana a Mulungu. Baibulo linanena choncho.

241 Munditche ine “woyera-wodzigudubuza,” ngati inu mukufuna kutero. Munditche ine chirichonse chimene inu mukufuna kutero. Malingana ngati mtima wanga uli bwino ndi Mulungu, ndipo chondichitikira changa chikugwirizana ndi Baibulo la Mulungu, ine ndikusuntha patsogolo pomwe mu mbali yomwe iyi. Inde, bwana. Ndicho chimene ife timakhulupirira. Ndiwo Mpingo wa Mulungu wamoyo, umene sumabwera mwa zamulungu. Iwo suwumabwera mwa lingaliro lina laluntha, lopangidwa ndi munthu. Iwo umabwera mwanjira ya mwamtheradi ndi Choonadi chowululidwa kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu.

242 Ngati ine ndingokhala nalo chabe lingaliro lamwaluntha, chifukwa mpingo wa Baptisti kapena mpingo wa Methodist unandiphunzitsa ine kuti zinthu izi *nzakuti-ndi-zakuti*; pamene ine ndilimva Baibulo ili, ngati Baibulo... Ngati ine ndikanakhala nditabatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” ndipo nditawerenga Baibulo ili, ndipo mlaliki nkundiwuzwa ine kuti apo panalibe wina aliyense mu Baibulo anabatizidwapo koma mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo ine nditawerenga izo ndi kuwona kuti icho chinali Choonadi, ine ndikanathamangira mu madzi mwaliwiro monga ine ndikanathera. Inde, bwana.

243 Ngati winawake akanandiuza ine kuti—kuti Yesu Khristu anali mchiritsi wamkulu; ndipo mpingo wanga ukanandiwuzwa ine kuti, “Masiku a zozizwitsa anapita,” ndipo ine ndikanakhala nako kusowa kwa machiritsi; ine ndikanathamangira

mwaliwiro basi monga ine ndikanathera, kupita ku guwa, kuti ndikakhoze kuchiritsidwa. Ine zedi ndikanatero.

<sup>244</sup> Ngati ine ndikanakhala mlaliki, ndipo ndikanakhala naye—mlaliki wamkazi mu guwa langa, ndipo ine nditawerenga mu Baibulo ilo ndi kuwona kuti mkazi samayenera kuti azilalikirira, ine ndikanamuchotsapo iye pamenepo, ngakhale izo zikanachotsa chikopa pa nsana wanga.

<sup>245</sup> Ndipo kumbukirani, nditakhala kumbuyo komwe kumene Mlongo Wright aliko, usiku wina, kuti mkazi ankati andiponyere ine kunjja kwa chitseko chifukwa chochita chinachake chonga icho. Inde, bwana. Ine ndinati, “Inu simubwera mu tchalitchi changa ndi zakale zanu. . .” Pamene iwo ankakonda kuvala, kapena kudula madiresi awo cha mmusi monga chonchi, ndi chinthu chowoneka-moseketa icho, ndipo pafupi theka la thupi lawo liri poyera. Ine ndinati, “Iwo akanati abwere mu mpingo wanga, ine zedi ndikanawatulutsa iwo kunjja.” Ndipo shasha wina wamng’ono wakale kumusi kuno, iye anafa osati kale litali zitachitika zimenezo; ndipo iye anandiyitana ine, akufa. Iye anali msungwana wa Katolika, anayenda kupita kumeneko ndipo anakhala pansu ndi izo monga choncho. Ine ndinayang’ana kumbuyo ndipo ine ndinamuwona iye, atakhala muno, ndipo iwo anali akuyimba. Ndinavula chikhotho changa, ndinayenda kupita kumbuyo kumeneko, kuchiyika icho mozungulira mapewa ake. Ine ndinati, “Madamu, ngati inu muti mumvetsera kwa ine ndikulalikirira, chonde mungavale chikhoto ichi pamene inu muli mu tchalitchi cha Mulungu.” Mwaona? Zedi.

<sup>246</sup> Iye anavundumuka kuchoka pamenepo, ndi kuwonetsa milomo yaying’ono iyo. Iye anapita kunjja kwa nyumbayo. Iye anati, “Ngati iye ali nacho chipembedzo, ine sindikanayilola ng’ombe yanga kukhala nacho chipembedzo cha mtundu umenewo.”

Ine ndinati, “Musati mudandaule, iye sadzakhala nacho icho.”

<sup>247</sup> Ndiye ife tinali ndi hema, iwo anandiyitanitsa ine pamene iye anali kumwalira. Iye anali ndi vuto la mtima, ndipo iye anali kufa. Mwamuna wake anabwera. Iye anati, “Bwerani mofulumira!” Ndipo ine ndinali mu msonkhano kumene. Mnyamata wamkulu, wamtali, atayima pa chitseko, akundiyeembekezera ine. Ndipo ine ndinathamanga pamene. . .

<sup>248</sup> Ine ndinalowa mugalimoto yanga ndipo ndinathamanga kupita kumeneko. Pamene ine ndinkapita mmwamba, ine ndinakomana naye namwino wakale uja wa kumeneko, yemwe ankakhala uko mu Howard Park, pamenepobe. Iye anati, “Abusa, palibe chifukwa chobwerera mkati.” Izo zakhala pafupi zaka makumi awiri zapitazo, mwinamwake pang’ono mochulukira. Anati, “Iye wafa.” Anati, “Iye wakhala atamwalira



kwa pafupi maminiti atatu.” Anati, “Iye anakulirirani inu, molimba monga iye akanathera kutero.” Anati, “Ine ndiri ndi uthenga wa inu.”

Ndinati, “Chiyani?”

<sup>249</sup> Anati, “Mumuwuze mlaliki ameneyo, za zomwe ine ndinanena, ‘Chonde andikhululukire ine.’”

<sup>250</sup> Ine ndinapita kumeneko kukayang’ana pa iye. Mkazi wokongola; ndipo iye anali atavutika molimba kwambiri. Iye anali ndi mabanga aang’ono cha pa mphuno yake; mkazi wokongola. Ndipo mabanga, ankawoneka ngati, anatulukira kunja. Ndipo maso ake anali atakankhika kwathunthu kutuluka mu zibowo, ndipo anali mwa theka atatembenezukira mmbuyo. Zoono, zammimba yake ndi chikodzodzo zinali zitayenderera, ndipo nthuzi inali ikubwera ponseponse pa bedipo, monga choncho.

<sup>251</sup> Ndipo mwamuna wake anayang’ana pa ine, anati, “M’bale Branham, nenani pemphero, chifukwa iye amafuna kuti akuwoneni inu.”

Ine ndinati, “Pemphero kwa iye tsopano silichita bwino ayi.”

<sup>252</sup> “Kumene mtengo umatsamira, ndiko kumene iwo umagwera.” Mukuona? “Musati mukhale onyengedwa; Mulungu sanyozedwa. Chirichonse chimene munthu amafesa, chimenecho iye adzachikolola.”

<sup>253</sup> Kodi inu mukuona pamene icho chiri? Tsopano ndi chiyani chachitika? Yang’anani pa mkazi amene ati adzachite zimenezo. Yang’anani pa akazi amene anakhalapo mmbuyo kutaliko, msungwana wa makolasi, kodi mwana wake wamkazi anali chiyani? Wadama. Kodi mwana wamkazi wa wadama ndi ndani? Wa kwasakwa mongopitirira zaka khumi. Kodi mwana wake wamkazi adzakhala chiyani? Nhu! Ndi chiyani icho?

Mwayiwona mbewu ya wolungama?

<sup>254</sup> Yang’anani Abaptisti anu. Pitani mmbuyo kanthawi pang’ono kapitako. Pitani mmbuyo kwa John Smith, woyambitsa wanu, inu Abaptisti. Pamene, iye anapemphera chifukwa cha kusayeruzika kwa anthu, mpakana, iye analira ndipo anapemphera chifukwa cha anthu mpaka maso ake anatupa motsekeka, ndipo mkazi wake ankachita kumamudyetsa iye pa gome, kadzutsa wake.

<sup>255</sup> Ndipo inu Amethodisti ozungulira pano, muli ndi ndolo mu mphuno zanu ndi pa makutu anu, ndi kuwoneka ngati zishyalozambali za mdierikezi; ndi kumapita kunja, mutavala akabudula, ndi zinthu monga choncho! Pamene, John Smith wakaleyo, mmodzi wa aakulu a mpingo wa Methodisti, iye asanafe ali wa usinkhu wa zaka makumi asanu ndi atatu mphambu zisanu, analalikira ulaliki waufupi zaka zinai... maora anai. Iwo anachita kumunyamula iye ndi kumukhazika

iye mu guwa. Ndipo awa anali mawu ake otsiriza. Iye anati, “Ine ndadzidzimuka pa zochita za mpingo wa Methodist.” Anati, “Ngakhale ana aakazi a mpingo wa Methodist akuvala mphete za golide pa zala zawo.” Kodi iye akananena chiyani tsopano, atavala akabudula, akuyimba mu kwayara?

<sup>256</sup> Inu munathamanga bwinodi. Ndi chiyani chinachitika? Inu mukuchita ngati mayi wanu. Ndizo chimodzimidzi izo.

<sup>257</sup> Ndicho chifukwa ife sitikufuna chirichonse cha zipembedzo izi kukhala pozungulira ichi, kapena kunyamulidwira kuno, “Ife ndife Amethodisti. Ife ndife Abaptisti.” Ife ndife chabe a Khristu. Zisiyeni izo mwa njira imeneyo, kukhala afulu.

<sup>258</sup> Tsopano, mwayiona mbewu ya serpenti? Kodi mkazi woteroyo akanalipira chiyani tsopano? Kodi icho chikanachita chiyani? Chiyani? Iwo anapitirizabe, kubwera mpaka mmusi. Iwo anakankhira Abaptisti kumbuyo, anakankhira Amethodisti kumbuyo, kukankhira Apresbateria kumbuyo. Iwo akanachita chiyani? Iwo onse anapita mmbuyo kumbuyo, monga mayi wawo, wachiwerewere wakale. Kumeneko iwo onse ali, akuchita chiwerewere chomwecho. “Chabwino, izo sizimapanga kusiyana kulikonse. Iwo amizidwa kale. Iwo akonkhedwa kale. Iwo, iwo abwera, apanga kuvomereza. Iwo atenga kudziletsa kwawo kwa miyezi isanu ndi umodzi; iwo sanamwe mochuluka kwambiri pa nthawi imeneyo, zina zotero. Iwo anakhala mamembala abwino. Iwo analipira bwino pa...” O, mai! Izo ziribe kanthu koti kachite ndi zipatso za Mzimu.

<sup>259</sup> Zipatso za Mzimu ndi “chikhulupiriro,” kukhulupirira Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse; “chikondi” cha pa abale; “chisangalalo, mtendere, kupilira-motalika, ubwino, ulemu, chipiriro, kufatsa, kudziletsa.” Ndizo zinthu zake, zipatso za Mzimu.

<sup>260</sup> Ndipo ife timamutenga munthu, “Chabwino, iye—iye amakhala moyo wabwino kwa oyandikana nawo.” Chomwechonso ankachita Esau.

<sup>261</sup> Esau sanamupweteke aliyense ayi, ndipo Esau anali wa mdierekezi; koma Yakobo, kuchokera mu mimba yomweyo, anali wa Mulungu. Mbewu ya mdierekezi; Mbewu ya mkazi, Mbewu ya Mulungu inabwera kupyoleramo.

<sup>262</sup> Tsopano, inu mukuwona, izo zonse zafika mmusi kwa ichi, ndi kwa chiyani kumene icho chatsalira mu dziko lero? Ine ndinena izi mwaukali kwenikweni, kukhomelera izi pansu, ndiye ife tiyamba chitsitsimutso zikatha izi, mu msonkhano wotsatira. Izo zafika pa mawonekedwe ake. Ndipo, chonde, ine sindikunena izi mosinjirira. Ine sindikunena izo kuti ndikhale wamwano. Izo zafika pa malo, ku gulu lachipembedzo, lalikulu la ana apathengo, a mchigololo. Iyo ndiyo ndemanga yanga yotsiriza. Ndicho chimodzimidzi chimene izo zafikako. Inu mukudziwa izo kuti ndi choonadi. Izo zafika pa malo mpaka ndi kujowina-

mpingo ndi mamembala a mpingo, “Okhala nawo mawonekedwe a umulungu, akumakana Mphamvu yake,” mpaka izo zafika ku gulu la achipembedzo, ana apathengo. Ndicho chimodzimodzi chomwe izo ziri.

<sup>263</sup> Ndi chiyani chotsatira chatsalira? Ilipo roketi imene yapachikika kutaliko, zingapo za izo, mabomba a kobalti ndi china chirichonse. Iwo akungoyembekezera mphamvu imeneyo kuti ifike. Ndipo pamenepo padzakhala chiwonongeko ndi moto, monga chinalipo ndi madzi.

<sup>264</sup> Ndipo, amzanga, chirichonse chimene inu muchita, ngati inu muli Mkhristu ndipo inu muli naye Mulungu mu mtima mwanu, ndipo inu mukudziwa kuti mwadutsa kuchoka ku imfa kupita ku Moyo, inu munayenera kukhala munthu wokondwetsa mu dziko lonse. Pamene Mzimu Woyera uli mwa inu . . .

<sup>265</sup> Pamene, Baibulo linanena kuti, “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse.”

<sup>266</sup> Zipembedzo zikunena kuti, “Koma ife tikukhulupirira kuti zozizwitsa ndi zakale.”

<sup>267</sup> Mzimu Woyera umati, “Ameni. Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, ndi kwa nthawizonse. Kotero zikhale izo.”

<sup>268</sup> Ngati Baibulo linena kuti, “Lapani, ndi kukhala obatzidwa aliyense wa inu mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku kukhululukira kwa machimo, inu mudzalandira Mzimu Woyera. Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi ana anu, kwa Amitundu, onse amene ali kutali, onse amene Ambuye Mulungu wathu—onse amene Ambuye Mulungu wathu ati adzawayitane!” Mwaona? (Osati, “onse amene Amethodisti adzawayitana, Abaptisti adzawayitana.”) Koma, “Onse amene Ambuye Mulungu wathu ati adzawayitane, adzalandira Mzimu Woyera uwu, ndi kukhala atabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu.” Ndicho chimene Baibulo linanena.

Pamene icho chikugundani inu, inu mumati, “Ameni.”

Mpingo unati, “O, izo sizipanga kusiyana kulikonse.”

<sup>269</sup> Koma Mzimu Woyera uwu mwa inu, ukuti, “ameni” kwa Mawu Ake. “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Ndi zimenezotu inu.

<sup>270</sup> Ine ndikufuna inu kuti mundisonyeze ine Lemba limodzi pamene ilo linayamba lanenapo kuti apulo inayambitsa chinthucho kuchitika tsopano. Ine ndikufuna inu kuti mundisonyeze ine kuti iwo anadya maapulo. Ine ndikusonyezani inu izo pamene Kaini ankaganiza chinthu chomwecho, ndi pamene mbewu yake ikanali kuganizabe chinthu chomwecho.

<sup>271</sup> Koma vumbulutso lauzimu la Mulungu limatsimikizira, mwa Baibulo, kuti iko kunali kugonana pakati pa mwamuna ndi mkazi, mosalodwa. Apo ndi pamene zimphona zanu

zinachokerapo. Ndi pamene tchimo lanu linachokerapo. Ndi pamene chivundi chanu chinachokerapo. Ndi pamene izo zachokera uko.

272 Tsopano zindikirani mu zonse izi—izi, penyani, s—serpenti anali wanzeru pawiri. Mbewu yake yakhala nthawizonse yanzeru pawiri. Ndipo ine ndikanakonda kukwera pamwamba pa guwa ili ndi kugwira choyankhulirapo ichi mu dzanja langa, [M'bale Branham akusuntha choyankhulirapo—Mkonzi.], ndi kuponda phazi langa pa guwa, ndi kunena izi. Ndipo, lero, alikuti aluntha anu aakulu? Abusa anu amene apita uko ndipo atenga luntha lochuluka la chidziwitso, ndipo iye akuyimirira; iye ali m'busa wa mipingo yayikulu kwambiri imene ilipo mu dziko, ndi zina zotero monga choncho. Kodi mbewu ya serpenti ikuyima kuti? Mu malo anzeru mwaluntha monga choncho; anzeru, masikolola othyathyalika. Apo ndi pamene iye ali. Ndi pamene iye akugona.

273 “Osati mwa mphamvu, osati mwa nyonga, koma mwa Mzimu wanga, atero Ambuye.” Mwaona? Apo ndi pamene inu . . .

274 Ndiye inu mumutenge m'bale wamng'ono atayima uko pa ngodya, akulira maso ake atatuluka, ndipo mwinamwake atayima uko akukhwatsha bangwe wachikale, akuti, “M'bale, bwera, dzapeze Ambuye!” [M'bale Branham akugogoda pa guwa kamodzi—Mkonzi.]

275 Abusa akuyendera kumeneko, nkunena, “Nhum! Sungakhale ndi osonkhana anga . . . Bwanji, ine sindikanayanjana, sindikanawalola anga . . . sindikanalola Liddy ndi Johnny ndi iwo kuti andiwone ine pozungulira malo otero ngati amenewo.” Pitirirani, mbewu ya mdierekezi, iwe walunjika kopita kwako kwa Muyaya, mulimonse. Ndiko kulondola. Ine ndikanakhoza kunena mawu ena pamenepo, ndipo ndikanati “mwana wa mchigololo,” ndipo ndi pafupi basi ndi pamene izo ziri. Pakuti, inu mukuona, inu . . .

276 “Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye. Ndipo onse amene adza kwa Ine, Ine ndidzawawukitsa mu tsiku lotsiriza. Pamenepo sipadzakhala kanthu kati kadzatayike. Ine ndiri nacho icho. Ine ndichisunga icho. Palibe munthu angakhoze kuchita izo, kupatula Ichi.”

277 Zonse zagona mwa Iye. Inu simungakhoze kunena kuti, “Ine ndinachita chinthu chimodzi.” Ndi chisomo cha Mulungu chimene chinachita izo zonse. Kotero, palibe chimene ine ndachita. Ine ndinalibepo konse kanthu koti ndichite; inu simunachitepo, ngakhale. Inu simunayenere kanthu kamodzi. Mulungu anachita chidutswa chirichonse cha izo. Inu simunatembenuze chala chimodzi chifukwa cha gawo limodzi la icho. Inu simunati, “Chabwino, ine ndikuchokera ku banja labwino. Ine ndinachita izi.” Izo chiribe chinthu chimodzi

chochita ndi icho. Mulungu ndi Mmodzi Yemwe anachita izo; chifundo cha Mulungu.

278 Ine ndikupepesa tsopano, iyo siiri kwenikweni leveni koloko, koma ine ndati nditseke, mulimonse. Mwaona?

279 Ndi angati akumvetsa kuti Baibulo limayankhula za zinthu izi kuti ndi Choonadi; inu anthu a pa Branham Tabernacle, makamaka? [Osonkhana anati, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano, ndizo pafupi gawo limodzi la khumi asanu ndi amodzi chabe la zimene ife timaphunzitsa ndi kukhulupirira. Koma, kumbukirani, kwa inu oyima mmbali, ine ndikhoza kunena ichi, inu anthu amene simumabwera kuno ngati membala. Momwe ife timakhulupirira izi, kuti *Ili* ndi Baibulo, ndipo Baibulo ndilo Choonadi cha Mulungu.

280 Ndipo ife timakhulupirira, kuti, mu Chipangano Chakale, tsopano, iwo anali nayo njira yodziwira chimene chinali choonadi ndi chimene sichinali choonadi.

281 Tsopano, ife tonse tikudziwa kuti iwo anali nalo lamulo lolembedwa. Ndi angati akudziwa zimenezo? Lamulo, ma—malangizo anali mu likasa, ndi zina zotero; chabwino, ndi lamulo pa malangizo. Anati, “Iwe usadzachite chigololo. Yense ati azichita chigololo kugendedwa.” Mukuona? Ilo linali—langizo, ndi lamulo pa malangizo. Tsopano, likasa linali kukhala monga *chonchi*; malangizo anali pansu mmenemo, ndipo malamulo a malangizo anali mu matumba cha pa mbali ya likasa. Ngati munthu abwera pansu apa, atachita chigololo; ankafika kuno ndipo ankatenga chimene lamulo linati, “muzimugenda iye.” Iwo ankamutengera iye kunja ndi kukamugenda iye. Ndicho chimene lamulo linali pa malangizo.

282 Tsopano iwo anali nazo njira zina ziwiri kuti adziwe. Pakhala nthawizonse pali zitatatu, ngati chitsimikiziro. Iwo anali nayo njira yina yodziwira, ndipo iyo inali mwina mwa mneneri kapena wolota. Ndi angati amene akudziwa zimenezo? “Ngati akhalapo mmodzi pakati panu yemwe ali wauzimu, kapena mneneri, Ine Ambuye ndidzadzawonetsera Ndekha kwa iye mu maloto, ndi kuyankhula kwa iye mu masomphenya.” Ndiko kulondola. Tsopano, iye anali wonenera.

283 Tsopano, kuti munthu abwera pozungulira, nati, “O, aleluya, ine ndachipeza icho! Ine ndikulosera tsopano mu Dzina la Ambuye. Ine ndiri nalo vumbulutso.” Iwo samalola icho kumachitika monga choncho, monga inu anthu mumachitira. Iwo amafufuza izo ndi Mulungu, choyamba.

284 Tsopano, pa chapachifuwa cha Aaroni iwo anali nacho chimene iwo ankachittha Urimu Tumimu. Ndi angati anayamba amvapo mawu amenewo? Chinali chiyani icho? Chinali miyala khumi ndi iwiri, isanu ndi umodzi pa mbali iliyonse, ya mbadwa khumi ndi ziwiri; jasi, Yuda, ndi ena otero, ndipo mpaka pansu, miyala khumi ndi iwiri. Ndiyeno iwo ankamutenga mneneri

uyu, kapena wolota, ndipo iwo ankapachika chapachifuwa ichi mmwamba, ndipo iwo ankamuyimika iye pamenepo. Ndipo iwo amati, “Tsopano losera ndipo nena ulosi wako.”

“Ambuye anayankhula kwa ine ndi kunena zinthu zakuti-zakuti.”

<sup>285</sup> Ziribe kanthu momwe izo zikuwoneka ngati zenizeni, izo zikhoza kumveka ngati basi zoonadi mwangwiro; koma ngati nyali izo sizinabwere palimodzi ndi kupanga mtundu wa utawaleza chodutsa pamenepo, Urimu Tumimu, nyali zimenezo zikuwundana palimodzi, kugwira ntchito kwauzimu, kukutsimikizira. Onani, Mulungu nthawizonse amatsimikizira Mawu Ake. Mukuona? Ndipo ngati nyali zauzimu izo sizinathwanimire pamenepo, ndiye ine sindikusamala kuti icho chimawoneka ngati chenicheni motani, icho chinali cholakwika.

<sup>286</sup> Ngati wolota anati, “Ine ndinalota loto, ndipo loto ili linanena, kuti, ‘Israeli ayenera kusuntha ndi kupita ku malo ena ake, chifukwa Asiriya abwera nadzalowa ku mbali *iyi* kuzinga kumeneko.’” Iwo ankamutengera wolotayo uko; iye ankanena loto lake. Ngati nyali izo sizinali kuthwanimira chodutsa pamenepo, iye anali wolakwitsa, ziribe kanthu momwe. . . Ngati Asiriya anali atakhale kale mu nkondo kutsidyalo, iye anali kulakwitsa. Ayi, bwana. Iwo, mwamtheradi, izo zinkayenera kuti zitsimikiziridwire ndi Urimu Tumimu.

<sup>287</sup> Tsopano aliyense akudziwa kuti unsembe wakale unapita, unathetsedwa, ndipo Urimu Tumimu anapita limodzi nazo izo. Ife tikudziwa zimenezo, sichoncho ife? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>288</sup> Ndipo unsembe watsopano unali kubwera mkati. Nchiyani? Kodi ife tiri nayo Urimu Tumimu lero? Inde, bwana. Mawu a Mulungu! Inde, bwana. *Ili* ndilo iyo. [M’bale Branham akusonya Baibulo lake—Mkonzi.] Ngati munthu aliyense ali nalo vumbulutso la mtundu uliwonse, kapena ayankhula chirichonse, kapena chiphunzitso chirichonse chimene sichiri molingana ndi ku- . . . ndi kugwirizana ndi Baibulo ili, kupyolera mu Lemba lonse, iye ali kulakwitsa. Ine sindikusamala chipembedzo chanji iye ali, iye ndi wabwino bwanji, iye ndi wanzeru bwanji, iye ndi wophunzirira bwanji; iye ali kulakwitsa.

<sup>289</sup> Ndipo pamene munthu aliyense akuwuzani inu zinthu izi, zimene ife taphunzitsa muno mu tchalitchi tsopano, ndi kukuuzani inu, kuti, “Ngati inu mwakonkhedwa kuti, izo ziri bwino basi,” iye wakuuzani inu bodza. Izo siziwalira pa Urimu Tumimu. Pamene iye akuwuzani inu, kuti, “Kutsanulira ndi kwabwino,” iye wakuuzani inu bodza. Iye akakuuzani inu kuti, “Kubatizidwa mu dzina la ‘Atate, Mwana, Mzimu Woyera,’ ndi kwabwino,” iye wakuuzani inu bodza. Ngati iye akuuzani inu, “Masiku a zozizwitsa anapita,” iye wakuuzani inu bodza. Ngati iye akuuzani inu, “Ndi zabwino kuti akazi azilalikirira,” iwe

wakuuzani inu bodza. Ngati iye akuwuuzani inu, “Ziribwino kuti inu muzipitirira ndi kukangamira ku chipembedzo chanu,” iye wakuuzani inu bodza. Izo siziwalira pa Urimu Tumimu. Ndipo madazeni a zinthu zimene zatuluka kuchokera, mwa wamkuluyo “MAYI WA KAHULE,” ndi kubwera mpaka uko, ndipo apo pali chifukwa chimene ife timakhala kutali ndi chipembedzo.

<sup>290</sup> Ife timawakonda abale athu ndi alongo kunja mu zipembedzo zimenezo. Koma inu musamati muzipita, ndi kumanena, “Ine ndine wa Methodisti,” ndi kukukhalitsani inu Mkhristu, kwa ine. Ndinu Mkhristu chifukwa inu mwabadwa ndi Mzimu wa Mulungu. Inu simusowa kuti mukhale wa Methodisti kapena wa Baptisti. Inu simusowa kuti mukhale chimodzi chirichonse. Inu muyenera kokha kuti mubadwe mwa Mzimu wa Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>291</sup> Pa makhazikitso awa, ngati aliyense ali pano ndipo akufuna kuyanjana ndi kubwera mu chiyanjano cha kupembedza uku, ndipo akufuna kuti akhale—akufuna kuti amizidwe, kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, pano pali dziwe. Iwo abatiza, mu miniti chabe.

<sup>292</sup> Ngati alipo wina, ambiri pano, aliyense amene akufuna kuti abwere, mwa njira ina iliyonse? Ife tiri pano. Ndiko kulondola.

<sup>293</sup> Tsopano, ife—ife sitikhala nawo umembala uliwonse; inu muzingobwera kuno ku mpingo uwu. Ife timakhulupirira kuti Khristu ali mu mpingo wa Methodisti, mpingo wa Baptisti, mpingo wa Presbateria. Iye ali nawo mamembala mu umodzi uliwonse wa iyo. Ndipo chimene chikuperewera, lero; ndi uneneri wabodza ukubweretsa zinthu izo poyera, kuphunzitsa kwa mipingo imeneyo, kumene kuli mwamtheradi kosiyana ndi Baibulo.

<sup>294</sup> Tsopano, ngati winawake akanapanga Izo kumveka chotero kwa ine, ine ndithudi ndikanadzitengera ndekha... Ine ndikukhulupirira kuti ulipo Mzimu wa Mulungu wokwanira mwa ine, kuti ndikafufuze mu Baibulo ilo ndi kubwera kuti ndidzakonze izo bwino. Ngati ine ndinangoyenda kupita ndi kukagwirana naye chanza mlaliki, ndi kuyika dzina langa pa bukhu, ndi kumakhalabe nawo udani ndi kuyipidwa mu mtima mwanga, ndi kumakhalabe nako kudukidwa ndi ndewu, ndi kusamakhulupirirabe Yesu Khristu kuti ndi mchiritsi wamkulu, ndi zina zotero monga choncho, ine ndikanapita ndi kukaziwongola ndi Mulungu, mwamsanga kumene. Ine zedi ndikukhulupirira kuti ndikanatero. Ine—ine ndikanakhala woona chotero pa izo. Ine ndikanapita ndi kukakonza bwino ndi Mulungu. Ngati ine ndikanadzipachikabe chifukwa ine ndinali wa Baptisti kapena Methodisti, ine ndikanapita uko ndi

kukatengera Chikhristu mu mtima wanga. Ine ndikanachita izo. Inde, bwana.

<sup>295</sup> Tsopano kumbukirani chitsitsimutso chikudzachi, chimene chiti chidzayambike, Ambuye akalola, Lachitatu likudzali usiku. Ndicho cha pa zikhazikitso izi.

<sup>296</sup> Mvetserani, amzanga, alipo Mulungu woona ndi wamoyo. Ndiko kulondola. Yesu Khristu ali Mwana wa Mulungu. Mzimu Woyera uli mu Mpingo lero.

<sup>297</sup> Tsopano, ngati ine ndikanangokhala naye winawake woti andiuzze ine zimenezo, ine ndikanakhala nawo ufulu woti ndikayikire zimenezo. Koma, mvetserani. Tsiku limodzi kutsidyako, ngati mnyamata wamng'ono, ine ndinali nditayima pansi pa mtengo, ndipo ine ndinamuwona Iye. Ine ndinamumva Iye. Iye anandiwuza ine, anati, “Khala kutali ndi akazi oyipa awo. Khala kutali ndi ndudu. Khala kutali ndi kutukwana, kumwa, ndi zinthu zonse izi. Ine ndiri nayo ntchito ya iwe kuti uyichite pamene iwe uti udzakulirepo.” Ine ndikudziwa Iye ndi weniweni, Mulungu wamoyo amene amagwirizana ndi Mawu Ake.

<sup>298</sup> Pamene ine ndinakhala wokulirapo pang'ono, momwe Iye anakomanirana nane ine, momwe iye anayankhulira kwa ine! Momwe ine ndamuwonera Iye kutsidyako, ngati chitsamba choyaka, ndi Moto umenewo ukusuntha chozungulira kutsidya! Momwe ine ndamuwonera Iye akuyankhula ndi kunena chimodzimodzi basi chimene chikanati chichitike; ndipo, nthawi iliyonse, kugunda mwangwiro monga momwe izo zikanakhoza kukhalira, mwangwiro monga choncho.

<sup>299</sup> Mmodzi yemweyo amene amanena zinthu zaungwiro izo monga choncho, ndi Mmodzi yemweyo Amene amandidzoza ine kuti ndiziphunzitsa Baibulo ili basi mwa njira imene ine ndimaliphunzitsira Ilo. Ndiko kulondola. Kotero, Izo zimabwera kuchokera kwa Mulungu. Kwa ine, ndi Mulungu Wamphamvuzonse, ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.

<sup>300</sup> Yesu anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Atate, ndipo ine ndikupita kwa Atate.” Pamene Iye anabwera . . .

<sup>301</sup> Pamene Iye anali Mulungu mu chipululu, Iye anali Kuwala koyaka. Ndi angati amene akudziwa zimenezo? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye anali Kuwala koyaka, Lawi la Moto.

<sup>302</sup> Ndipo Iye anabwera kuno ku dziko lapansi, ndipo Iye anati, “Ine ndabwera kuchokera kwa Atate, ndipo Ine ndikupita . . . Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo Ine ndikupita kubwerera kwa Mulungu.”

<sup>303</sup> Pamene Iye anafa, kuyikidwa, nawuka kachiwiri, ndipo Paulo pamene anali pa njira yake akupita ku Damasiko anakomana nayenso Iye, kodi Iye anali chiyani? [Winawake



akuti, “Lawi la Moto.”—Mkonzi.] Akadalibe Lawi la Moto. Inde, bwana.

<sup>304</sup> Kodi Iye anachita chiyani pamene Iye anali pano pa dziko lapansi? Kodi Iye anachita chiyani pamene Iye anakomana naye Paulo? Kodi Iye anamutuma iye motani? Iye anamutumiza iye kwa mneneri amene anamuuya iye momwe angati abatizikire, anamuuya iye choti achite; anayika manja ake pa iye ndipo anamuchiza iye, anamuuya iye kuti anali atawona masomphenya.

<sup>305</sup> Yesu yemwe uja ali pano lero, akuchita zinthu zomwezo, ndipo akadali Lawi la Moto lomwelo, akuphunzitsa chinthu chomwecho, ndi kuchitsimikizira icho mwa Mawu Ake, ndi mwa zizindikiro ndi zodabwitsa. Ine ndiri wokondwa kukhala ndiri Mkhristu, ine sindikudziwa choti nkuchita. Ine ndiri wokondwa kuti inu ndinu Mkhristu.

<sup>306</sup> Ndipo inu, pa kachisi pano, ine ndinakuuzani inu kuti ife tisintha dzina la uyu. Izi siziri zokhoza kuti uyu akhale Branham Tabernacle. Ameneyo ndi munthu chabe, mukuona. Ife tilisintho dzina lakeli, kulipanga dzina lake lina. Ife tifika pa izo, pakapita kanthawi. Ine ndikungofuna iye kuti akhale m—mpingo wa Mulungu wamoyo. Ine sindikufuna iye akhale Methodisti, Baptisti, Presbateria, Pentekoste. Ine . . .

<sup>307</sup> Anthu onse awo, ine ndimawakonda ndi mtima wanga wonse. Ine sindikudziwa uti ndi uti. Ine sindingakhoze kukuwuzani inu. Ine ndikungoyenera kuti ndizilalikira Mawu. Ine ndimaponya ukonde ndi kukokera iwo mkati. Umo muli achule, ndipo umo muli akangaude ammadzi, ndipo umo muli njoka, ndipo umo muli nsomba zina, namonso. Izo ziri kwa Mulungu kuti alingalire pa izo. Ine ndimangokoka ukondewo, kumangolalikira Mawu ndi kuukokera iwo mkati, ndi kunena, “Ndi awa apa, Ambuye,ponse pozungulira guwali. Inu mukudziwa Inu Mwini; Inu munawadziwa iwo chikhazikitsireni maziko. Ine sindikudziwa chiti ndi chiti. Inu mukudziwa, kotero izo ziri ndi Inu, Ambuye. Ndicho chopambanitsitsa chimene ine ndikanakhoza kuchita. Ine ndipita kuno ndi kukaweza kwina kwake tsopano, ndi kukatengera gulu lina mkati. Ndicho chonse chimene ine ndingakhoze kuchita.” Chabwino.

O, ine ndikumverera ngati ndiziyendabe,  
Ine ndikumverera ngati ndiziyendabe;  
Kwathu kwa Mmwamba ndi kowala ndi  
kwabwino,  
Ndipo ndikumverera ngati ndiziyendabe.

<sup>308</sup> Tsopano kumbukira, aliyense amene akufuna zokambirana, ingowayimbirani Bambo Mercier kuno, kapena BUtler 2-1519. Ife tidzakhala okondwa kukuwonani inu. Ngati okondedwa anu akubwera, mukusowa kuti mufulumire kupita mu nthawi ya chitsitsimutso. . . Tsopano ine ndikupita, kuchokera pa

usikuuno, kupita kwa ndekha, ndi kukhala nditapita kwa masiku awiri tsopano, kwa ndekha.

<sup>309</sup> Ine ndikangolowa mkati mmenemo ndi kupita kukawerenga, monga chonchi, “Ambuye, Inu muli pafupi ndi ine. Ine ndikudziwa Inu muli pano. Ndipo Mawu Anu anati Inu mudzayandikira kwa iwo amene ayandikira kwa Inu.” Ine ndipitirira kumapemphera ndi kuyang’anira mpaka ine nditawona Lawi la Moto lija likuyamba kusuntha. Ine ndimadziwa kuti izo zakonzeka ndiye. Ndiye ine ndimayenda kulowa kupita ku nsanja ku utumiki wa machiritso, kuti ndikapemphere, ndi kuti ndikachite chimene ine ndingakhoze kuti ndiwathandize odwala ndi osautsika.

<sup>310</sup> Ife tikuyamikira chifundo chanu chonse tsopano. Ndipo pamene inu mukubwera, bwerani mukukhulupirira, ndipo ife tikuyembekezera kuti tikhala ndi msonkhano waukulu. Ine ndimafuna kuti ndinene izo . . .

<sup>311</sup> M’bale Jefferies, kodi iye ali pano usiku uno? Ife tikufuna kuti timuyamikire M’bale Jefferies ndi ntchito yake. Ine ndikuganiza iye wapita kubwerera ku zilumba, ndi kwina koteru.

<sup>312</sup> Ndakondwa kumuwona M’bale ndi Mlongo Wright, ndi ochuluka a anthu inu pano.

<sup>313</sup> Ndipo ine ndinamuwona wazamalamulo Robertson pano, kanthawi kapitako, anabwera mkati kanthawi kapitako. Ine ndimafuna kuti ndimuyamikire iye pa wake—pa uthenga wake umene iye anali nawo tsiku lina. Palibe amene ananena yemwe iye anali; ine ndinachita manyazi. Iye anali ndi uthenga wabwino kwenikweni pa ulosi, chinachake chonga chimene ine ndakhala ndikulalikira usikuuno.

<sup>314</sup> Ndipo, koteru, ndiye pamenepo panali mtumiki wina pano mmawa uno, kapena usiku watha, M’bale Smith, wochokera ku mpingo wa Methodisti . . . kapena wochokera ku mpingo wa Mulungu, cha kuno. Ine sindikudziwa ngati iye ali pano usikuuno, kapena ayi. Ngati inu mutangoti muyimirire pa guwa ili ndi kuyang’ana kumbuyo mbali iyo, zikukhala ngati ndi zovuta kuti udziwe; ndi kwa fulati, inu mukuona, ndipo iwe sungakhoze kudziwa. Ngati inu muli pano, M’bale Smith, ife tikuyamikira inu.

<sup>315</sup> Ndipo kodi si uyu, wakhala kumbuyo kuno, m’bale wamng’ono uyu wochokera ku Georgia, kumbuyo komwe kuno wakhala pambali pa M’bale Collins? [M’bale Neville akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Wokondwa kukuwonani inu kachiwiri usikuuno, m’bale.

<sup>316</sup> Ndi nonse a inu, nonse a inu, mmodzi aliyense mukudziwa yemwe inu muli.

317 Ine ndikukhulupirira uyu ndi mlongo ndi m'bale kuno amene anapita ndi kukamupempherera msungwana uja nthawi ija, komwe kuno, dokotala wakhala cha apa pambali. Ambuye akudalitseni inu, dokotala.

318 Tsopano, chonde musati mumverere mokhumudwitsidwa ndi ine, inu atumiki ndi abale, chifukwa cha momwe ine mosamalitsa ndikuwongololera izi mkati basi molimba monga ine ndingathere. Uyu ndi kachisi wathu. Ndi chimene ife timayima nacho, ndipo ife tikufuna kuchiyala Icho kumene pa Mawu amenewo, ndi kuwagwedeza iwo ndi Icho. Ndiye, ngati inu muti muchoke konse pa mzere, ife tidzabwerera ndi kuti, "Inu mumadziwa bwino. Ndi Izi ziri apa pa tepi." Mwaona? Ndi zimenezotu. "Ndi Izi ziri apa pa tepi."

319 Ife tiri nazo zochuluka zonse zina tiyenera kumapitiriza, ndiye, Leo. Koma, koma ife. . . Inu muli nazo zochuluka chotero. Inu mukhale mopitiriza ndi Izo, ndipo ife tidzatenga zonse za Izo pakapita kanthawi. Monga munthu amene anali, akudya chivwende, anati, "Icho chinali chabwino kwenikweni, koma ziripo zochuluka zina za izo." Kotero ife tiri nazo zambiri zochuluka za Izo, panobe, zikubwera.

320 Ambuye akudalitseni inu, kwenikweni mwabwino tsopano. Pamene ife. . . Timati tikhale ndi utumiki waubatizo pakali pano. Ndi kulondola uko, M'bale Neville? [M'bale Neville anena, "Eya, ine ndikukhulupirira choncho."—Mkonzi.] Kodi alipo winawake pano woti abatizidwe pakali pano? Ife sitikusamala yemwe inu muli; ife tiri—ife tiri pano kuti tibatize. Kwezani manja anu, iwo amene anali oti abatizidwe. Winawake, ine ndikukhulupirira iye anali. . . Pano pali dona pano. Ndipo kodi analipo wina aliyense? Tsopano, ife tiri nazo zovala kuno za onse amuna ndi akazi.

321 Tsopano, ife sitikunena kuti, "Siyani mpingo wa Baptisti. Siyani mpingo wa Methodisti." Ife sitikunena choncho. Inu pitani mubwerere kumene ku mpingo wanu. Koma ngati inu simukhala muli obatzidwa molingana ndi Lemba, mu Dzina la Ambuye Yesu. . . Osati mu Dzina la "Yesu" lokha, tsopano. Mu Dzina la "Ambuye Yesu Khristu," ndilo Lemba. Inu mwabatizidwa molakwika.

322 Ine sindikufuna vuto ayi pamene ine nditi ndikafike pa mtsinje. Ine ndikufuna chirichonse bwino bwino monga ine ndikudziwira kachitidwe kache, pamene ine ndiri kugwirizira chiphatso icho, mukuona, chifukwa ine ndikufuna kuti ndidzakwere pa icho nthawi imeneyo. Ine ndikanakulangizani inu kuti muchite mofanana.

323 Bwererani mupite ku mpingo wanu. Izo ziri, pakati pa inu ndi Mulungu. Ndizo zonse zimene ine ndingakhoze kukuuzani inu.

324 Koma palibe mmodzi mu Lemba anayamba wabatizidwapo mwa njira ina iliyonse koma Dzina la “Ambuye Yesu Khristu.” Ndipo iwo amene anabatizidwa, analamulidwa ndi Paulo Woyera, yemwe anati, “Ngati Mngelo akanalalikira chinthu china chirichonse, msiyeni iye akhale wotembereredwa.” Anawalamulira iwo kuti abwere ndi kudzabatizidwa, kachiwiri, mu Dzina la “Ambuye Yesu Khristu.” Ndiko kulondola. Ndipo iye anachita izo. Ndipo zomwe iye anachita, iye anatilamulira ife kuti tizichita; ndi zomwe ife titi tizichita, Mulungu akalola.

Ife timakhulupirira mu kutsukana mapazi. Ife timakhulupirira mu mgonero.

325 Ife timakhulupirira mu Kudza kwachiwiri kwa Khristu, thupi lenileni, losawoneka la Ambuye; osati Mzimu, koma thupi lenileni la Ambuye Yesu likubwera kachiwiri mu ulemerero.

326 Ife timakhulupirira mu chiwukitsiro cha thupi cha akufa, kuti alandire thupi, osati lakale ndi lamakwinya monga ife timapitira kumanda; koma lina latsopano, mu kukoma kumene kwa unyamata, kukakhala moyo nthawizonse.

327 Ife timakhulupirira mu chisavundi cha moyo, mwamtheradi. Ife timakhulupirira kuti alipo mawonekedwe amodzi okha a Moyo Wamuyaya, ndipo ndiwo Moyo umene iwe umawupeza kuchokera kwa Khristu Yesu. Ndiko kulondola chimodzimodzi.

328 Chotero, ife sitimakhulupirira mu chilango Chamuyaya. Ife timakhulupirira mu moto wa gehena, mwalawasulfure ukuyaka, koma ife sitikhulupirira kuti iwo umayaka kwa nthawizonse; ngati iwo umatero, iwe uli nawo Moyo Wamuyaya. Pali Moyo Wamuyaya umodzi wokha; Umene umabwera kuchokera kwa Mulungu. Ndiko kulondola. Iwe udzakawotchedwa, mwinamwake kwa zaka milioni, zaka mamilioni khumi, ine sindikudziwa, koma iwe sungakhoze kukhala nawo Moyo Wamuyaya. Iwe sungakhoze kuyaka kwa nthawizonse. . . Iwe ukhoza kuyaka kwa nthawizonse, koma osati Muyaya. Mwaona, pali kusiyana pakati pa Muyaya ndi nthawizonse. *Nthawizonse* ndi nthawi za nthawi, cholumikizira, chikutanthawuza “danga la nthawi.” Koma, Muyaya, iwe sumakhala ndi chilango Chamuyaya.

329 Iwe uli nawo Moyo Wamuyaya, chifukwa alipo mawonekedwe amodzi okha a Moyo Wamuyaya. Ndipo iye amene ali nawo Moyo Wamuyaya, amakhala moyo ndipo ali wodalitsidwa ndi Mulungu kwa nthawizonse.

330 “Koma moyo umene umachimwa, moyo umenewo udzachita. . .” Chiyani? [Osonkhana akuti, “. . . kufa.”—Mkonzi.] Ndiko kulondola. Ndiye, iwo ulibe Moyo Wamuyaya. Ndithudi. Iwo uli—uli nacho chilango chake, koma osati Moyo Wamuyaya.

331 Kotero, inu mukuona, pali zinthu zambiri apobe zoti ziphunzitsidwe, ife tizipeza kanthawi kena. Ambuye akudalitseni inu.

332 Tsopano tiyeni tiyimbe nyimbo yakale iyi, pamene mlongo wathu akupita mkatimo. Ine ndikukhulupirira kuti dona uyu apa akhoza . . .

333 Rosella, kodi amenewo ndi amayi ako? [Mlongo Rosella Griffin akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Bwanji, adalitse mtima wanu! Wokondwa kukuwonani inu, mlongo, mukuchita zimenezo. Ndizo zabwino kwambiri.

334 Rosella Griffin, mmodzi wa abwenzi aang’ono abwino kwambiri amene ife takhala nawo. Iye ndi mkazi wamng’ono yemwe anali chidakhwa; kwa ena a inu anthu pano, akhoza kukhalapo alendo. Rosella samasamala ine kunena zimenezo. Pamene iye anabwera pa nsanja pamwamba apo pa—pamene . . . kumtunda kuno ku Indiana. Inu munayamba mwawonapo chiphakasa, iye anali mmodzi wa iwo, chidakhwa cholenguka maso. Kumene, madokotala aakulu anai a ku Chicago ananena kuti iye ali . . . Othandiza zidakhwa, ndi china chirichonsecho, anamulephera iye. Koma usiku umodzi pamene iye anabwera mu msonkhano, Mzimu Woyera unafukula moyo wake ndipo unamuza iye apo pomwe. Icho chinakhazikitsa zimenezo.

335 Yang’anani pa iye tsopano, ine ndikuganiza, usinkhu wa zaka makumi atatu-chinachake, anadutsa khumi zisanu ndi zitatu; wokondeka, mkazi wamng’ono wokongola. Sanalawepo kachasu chiyambireni; alibenso chikhumbo chake. Akukhalira moyo Khristu, akupita mozungulira mu misewu, kulikonseko, akuchitira umboni kwa ulemerero wa Mulungu, kwa ochimwa ndi zidakhwa, monse mu mipata ya matabwa, ndi china chirichonse, kupyola mu Chicago, akuchitira chinachake Ambuye.

336 Iye anabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu, ndipo mayi ake akubwera usikuuno kuti achite monga zomwezo; ngati Mulungu akanakhoza kumuchiza iye, ngati Yesu anakhoza kumuchiza iye . . . “Chirichonse chimene inu muchita mu mawu kapena mu ntchito, chitani izo zonse mu Dzina la . . .” [Osonkhana, “. . . Yesu Khristu.”] Ndicho chimene Baibulo linanena. Ndiko kulondola.

337 Chabwino, tsopano ife tikuti tikhale ndi utumiki wa ubatizo. Ife tizimitsa nyali kwa maminiti pang’ono pokha pamene ife tiri kukonzekera za utumikiwo, kuti abatizidwe, ndi—ndiyeno ife tikuyembekezera nthawi yabwino mwa Ambuye.

338 Kodi inu muchita utumiki wa ubatizo usikuuno? Chabwino, inu kulibwino—kulibwino inu mukonzekere. Ndipo ine ndiyambitsa, ine nditsogolera nyimbo ndi zinthu pamene ife tikupitirira ndiye. Pamene iwo akuko- . . . [M’bale Neville akuti, “Kodi ziripo zovala zirizonse kumbuyo kuno, Doc?”—Mkonzi.] Zovala za ubatizo, Doc, mwamsanga pompano. Chabwino.

339 Tiyeni tingoyimba imodzi ya zabwino zakale izi . . . [M'bale Branham akutsogolera kuyimba kwa osonkhana, pamene M'bale Neville akumubatiza mlongo—Mkonzi.]

340 [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Ndipo mpaka ife tizichita zimenezo, pamene ife tikuchoka, ife tiyenera kumachita chiyani?

Tenga Dzina la Yesu ndi iwe,  
Kugwa modzipereka pa mapazi Ake,  
Mfumu ya mafumu Kumwamba, tidzamuveka  
Iye korona,  
Pamene ulendo wathu watsirizidwa.

Chabwino, tiyime pa mapazi athu!

Tenga Dzina la Yesu ndi iwe,  
Mwana wosawuka ndi wa tsoka;  
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza iwe . . .

341 Ine ndikuuzani inu choti tichite. Tembenukani mozungulira ndi kugwirana chanza ndi aliyense pamenepo, ndi kunena, “Muli bwanji, m'bale? Ine ndiri woyamikira kwambiri kulumikizana ndi inu.”

Dzina lofunika, O lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha dziko ndi chisangalalo cha  
Kumwamba;  
Dzina lofunika, dzina lofunika, O . . .



*MBEWU YA SERPENTI* CHA58-0928E  
(The Serpent's Seed)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingerezi pa Lamlungu usiku Seputembala 28, 1958, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1996 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1996 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)